

Phunziro La Ziwanda

Dera Lachipembedzo



Ndikudabwa ndi angati amaidziwa nyimbo yaing’ono iyi, pamene ine ndikukupatsani inu moni wa chiyanjano cha Chikhristu ndi chikondi cha Khristu lero, ndi angati amaidziwa nyimbo yaing’ono iyi, “Iye Asamala Inu”? Inu mukuidziwa iyo? Chabwino, tiyeni tiwone ngati tingaipeze iyo. Inu mukuidziwa iyo, mlongo? Inu mukuidziwa? Tsopano:

Iye asamala inu,
Iye asamala inu;
Mkuwala kapena mthunzi,
Iye asamala inu.

Oh, izo ndi zabwino. Tiyeni tiyesere iyo kenanso tsopano.

Iye asamala inu,
Iye asamala inu;
Mkuwala kapena mthunzi,
Iye asamala inu.

[Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

² Atate athu Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu kuti Inu mumatisamalira ndipo mwawonetsera chikondi Chanu pa ife, mochuluka mpaka kuti Inu munatumiza Mwana Wanu wokonedwa, kuti...Mwana wa Mulungu wosalakwa, kuti adzatenge malo a ochimwa. Mmene ife tikukuthokozerani Inu, kuti Inu munatisamalira ife ndipo mumatiganizira ife, kuti munachita ichi! Ndipo ndife oyamikira kwambiri, Ambuye. Ife tiri okondwa kusunkhana pano masana ano, pansi pa madenga a mlengalenga, ndipo tikupempha madalitso Anu pa msonkhano uno. Perekani, Ambuye, kuti mwamuna aliyense, mkazi, mnyamata kapena mtsikana amene ali pano, awerenge mwakuya tsopano mu Malemba. Ife tikuyang’anizana ndi dziko limene likuyendetsedwa ndi Satana. Ndipo, Atate, ife tikupemphera, pamene ife tikuphunzira za mphamvu ya ziwanda ndi chimene izo zimachita kwa anthu, kuti Inu mutipatse ife chikhulupiriro chapamwamba, ndipo mulole zizindikiro zazikulu zambiri ndi zodabwitsa zichitike. Pakuti, ife tikupempha izi mu Dzina la Khristu ndi kwa ulemelero wa Mulungu. Amen.

³ Ife tiri, kuphunzira masana ano, mwamsanga tilowe mmenemo, ine ndikuganiza, pafupifupi maminiti fifitini molawirira. Tikadali pa *Phunziro La Ziwanda*.

⁴ Ndipo tsopano ine ndangolandira uthenga, kamphindi kapitako; M’bale Beeler, wochokera kwa azimzanga. Ndipo

ine ndikayambira mu Afrika, mkati mwa Julaye. Chotero izo zikukhazikitsa izo, ife tazikonza izo tsopano. Ndipo M'bale Baxter sangapite pa nthawi imeneyo, chotero ine ndikuyenera kuti ndidzapite ku Afrika ndekha. Chotero ndikupita kumeneko ndi . . . mulole . . . Inu mukuyenera mundipempherere ine tsopano, kuti Ambuye andithandize ine, chifukwa ine ndithudi ndiwasowa iwo tsopano, kumeneko pakati pa . . . Ine ndikuyembekezera pafupifupi anthu thuu handiredi sauzande mu msonkhano umenewo.

⁵ Ndipo ine ndiri ndi masomphenya atalembedwa apa. Ine ndikufuna anthu inu mupindule ndi iwo. Izo zinachitika mu Disembara. Ine ndinali mu chipinda mmawa wina pamene Mngelo wa Ambuye anabweramo. Ine . . . Inu mwaona, pamene ine ndinali kumeneko, ine sindinamumvere Mulungu, ndipo ine ndinakatangako ameba. Munthu aliyense amadziwa—amadziwa chimene ameba ali, kachiroambo kamene kamalowa . . . kamatsala pang'ono kukupha iwe. Ndipo chifukwa choti ine ndinachita chinachake chimene Mulungu anandiuza ine kuti ndisachichite. Ndi angati amene anamva nkhani ya izo? Ine ndikuganiza ena a inu muli pano. Ine ndikudziwa anthu ochokera pozungulira kachisi anamva nkhani ya chimene chinachitika. Mulungu anandiuza ine kuti ndipite ku malo, ndi kuti ndikakhale kutali ndi malo *awa*, ndipo kuti ndikabwerere ku malo ena. Ndipo ine ndinawalola alaliki kuti ayankhule zondichotsa ine mu izo. Tsopano, alaliki ndi opambana, ndipo iwo ndi abale anga, koma iwe uzisamala zimene Mulungu akukuza iwe. Uko nkulondola. Mukuona? Iwe uli ndi ntchito imodzi.

⁶ Ndi angati amene akukumbukira nthawi ina panali aneneri awiri mu Baibulo? Ndipo mmodzi wa iwo, Ambuye anamuuzwa iye, anati, “Iwe upite ku malo *enaake*. Ndipo iwe usati—usati ukabwere . . . Iwe ukabwerere kudzera njira ina,” ndi zina zotero. Ndipo—ndipo anati, “Iwe usakadye kapena kumwa pamene iwe ukakhale kumeneko.”

⁷ Ndipo mneneri wina woona anakumana naye iye, ndipo anati, “Ambuye anakumana ndi ine Iye atatha kukumana ndi iwe.” Ndipo anati, “Ubwere kunyumba kwanga.” Ndipo mneneriyo anamvetsera zimene winayo ananena, ndipo anataya moyo wake chifukwa cha izo. Mwaona, iwe uzichita chimene Mulungu wakuuzwa iwe kuti uchite mosalabadira zimene wina aliyense akunena.

⁸ Tsopano ife tiri . . . Mu masomphenya awa, Iye . . . Iwo anandidzutsa ine, pa sartini Seputem . . . kapena Disembara. Ndipo—ndipo pamene ine ndinali nditakhala mmphepete mwa bedi yanga, ine ndinali kudabwa kuti tsogolo langa lidzakhala lotani. Ine . . . Pamene ine ndinadzabwerera kuno, iwo anali okonzeka kuti andiponyere ine mu nyumba ya tizirombo, tizirombo tinangotsala pang'ono kuti tinditenge ine. Ndipo iwo

anandiyeza ine pamene ine ndinadzafika mdziko lino. Ndipo, mwa chisomo cha Mulungu, iwo anangondilola ine kuti ndizipita kwathu, chifukwa ito tinali titamwazikana kwambiri. Ndipo ndinapemphera, ndipo ndinapita kwa atumiki amenewo, ine ndinati, “Ambuye anena ndi ine kuti ndisapite njira imeneyo.”

Anati, “Oh, Mulungu amayankhula ndi ena pambali pa inu.”

⁹ Ine ndinati, “Korah anali ndi lingaliro limenelo nthawi ina.” Ndipo chotero, koma ine ndinapita ndipo ndinakatenga masamba ena ndipo ndinadzawayika iwo pa mapazi awo, ndipo ine ndinati, “Kumbukirani, mu Dzina la Ambuye, ngati ife titakhale ndi ulendo umenewo uko, iwo udzakhala wolephereka, ndipo ife tonse tidzalipira chifukwa cha izo.” Ndipo ndithudi ife tinatero! Oh, mai! Ife tonse tinakhala ngati tikufa. Chotero ndiye pobwerera . . .

¹⁰ Inu mumakhala ndi zochuluka zoti mulimbane nazo mmaiko akunja amenewo. Mwachitsanzo, utitiri waung’ono ukhoza kukulumani, ukhoza kukupangitsani inu kukhala ndi matenda a utitiri. Ndipo kanthu kakang’ono kameneko, pamene iko kakuluma iwe, ngati ukuzimva wekha kuyabwa, iwe sungakande. Iwe umayang’ana, ngati iko kali kanthu kakang’ono kakuda, usakachotsepo. Iko kamakhala ndi mutu waung’ono, iko kamaboola njira yake kulowa mu khungu, kamatembenuka monga *chonchi* ndi kukazimangitsa kokha. Ngati inu mungakakoke iko, inu mukhoza kukoka mutu mmenemo. Iko kamakhala ndi kachiroambo mkati mwake, kakhoza kupha ziwalo zako. Chotero iye. . . Osakanda, kapena osakokapo iko; umangotenga phula lina. Ndipo iko kamapumira kumbuyo kwake. Mukaika phula pamenepo, ndipo iko kamagwapo.

¹¹ Ndiye pali udzudzu waung’ono. Iwo sumapanga phokoso nkomwe. Iwo umabwera kudutsa mu mpweya. [M’bale Branham akumenyetsa dzanja lake—Mkonzi]. Iwo umangokukhudza iwe, ndizo zonse, iwe watenga malungo.

¹² Ndipo—ndipo kenako pali chimene amachitcha njoka ya mamba. Ngati iyo ikuluma iwe, iwe umangokhala pafupifupi maminiti awiri iyo itakuluma iwe.

¹³ Ndipo pali mphiri yachikasu. Iwe umakhala moyo pafupifupi maminiti fifitini iyo ikakuluma. Ndipo imodzi ya izo inali pafupi kwambiri ndi mwana wanga wamwamuna, pamene iye akanayika dzanja lake pa mutu wake. Itadzuka kale, kuti imulume, ife tisanaiwombere, monga choncho.

¹⁴ Ndipo kuli mphiri yakuda. Oh, kuli chirichonse basi! Ndiyenso zowopsya za kuthengo za nyama, ndithudi, mikango, nyalugwe, kapena akambuku, ndi china chirichonse zoti ulimbane nazo, mu thengo. Ndipo kenako matenda, kuli mitundu yonse basi ya matenda kumeneko.

¹⁵ Ndipo iwe umakhala nazo zonsezo zoti ukumane nazo pamene iwe ukupita. Pambali pa zimenezo, ndiye apa pali msing'anga woti azikutsutsa iwe mbali iliyonse, mwaona, ndi zamatsenga zawo zonse ndi zinthu. Koma, motani, ndi chinthu chopambana bwanji kuwawona Ambuye wathu akungozikankhira kutali, kuchokera kumbali kupita kumbali, monga choncho, kenako nkumapitirira.

Ndipo tsiku limenelo ine ndikukumbukira, nditaima pamenepo, mmene mwabwino, chimene chinachitika, ine ndidzakuuzani inu nthawiina mu msonkhano wina, chifukwa ine ndikufuna ndifike pa phunziro langa masana ano, la *Phunziro La Ziwanda*.

¹⁶ Koma tsopano, ndipo ichi ine ndinali kuchiganizira, nditakhala pamenepo, kodi mapeto ake akhala otani? Ndipo tikubwerera powoloka nyanja, ine ndikudziwa ife tinali ndi pafupifupi owatembenuza handiredi sauzande pamene ife tinali kumeneko. Ndipo M'bale Bosworth wokalamba anabwera kwa ine. Anati, ine ndinati, "Chabwino, M'bale Bosworth?"

¹⁷ Iye anati, "Ndine wonyadira kwambiri za inu, M'bale Branham!" Iye anati, "Inu basi—in u mwangokhala koyambirira kwa moyo," ndipo iye anatero.

¹⁸ Ine ndinati, "Chabwino, ine ndikuganiza izo zonse zatha." Ine ndinati, "Ine ndadutsa usinkhu wa zaka forte. Ine ndikuganiza ndamenya nkondo yabwino ndipo ndamaliza ntchito."

¹⁹ Iye anati, "Mwadutsa usinkhu wa zaka forte?" Anati, "Ine ndinali wa usinkhu umenewo ine ndisanatembenuke." Anati, "Ine ndiri bwinobe." Iye anali akuyandikira kuti azilowa mu maeyite ake. Ndipo basi. . .

Ine ndinaganiza, "Chabwino, mwinamwake izo ndi zoono basi."

²⁰ Chotero iye anati, "Ayi, inu mwangokhala Branham watsopano tsopano. Inu mumadziwa kayendetsedwe ka misonkhano yanu bwino, ndi chirichonse." Anati, "Basi ngati inu munayamba mwamumenyapo Amerika mwanjira yolondola, ndi msonkhano wokonzedwa molondola, pamene inu mungakhale kwa masabata sikisi kapena eyiti pa malo, ndi kuukonza iwo ndi kulengezetsa konsekonse," anati, "inu mukanachita chinachake, koma, ndi kwa Ambuye athu." Chotero ife tinapitirira, basi kumapitirira monga choncho, chotero izo zinali kwambiri—zabwino kwambiri.

²¹ Kenako patapita kanthawi, ine ndinawona masomphenya, pamene ine ndinali ku Amerika, ndipo iwo anabwera kwa ine, ndipo anandibweza ine ku Afrika, ndipo iwo anandiwonetsa ine msonkhano womwe uja, nditakhala pamenepo kutsogolo kwa Durban. Ndipo msonkhano woyamba unazimilira kupita mu mbiriyakale, kupita moloza cha Kumadzulo. Msonkhano

wachiwiri unabwera ndipo, pamene iwo unatero, iwo unali waukulube kuposa mmene msonkhano woyamba unaliri. Ndipo Iye... Ine ndinamva kufuula, ndipo Mngelo anali akubwera kuchokera Kumwamba; Iye anali ndi kuwala kwakukulu.

²² Ndipo Mngelo wa Ambuye amene anaima pafupi ndi ife apa, anali atayi... nthawizonse amayima kumanja kwanga, cha kumbali *iyi*. Ndipo Iye anali atayima pamenepo, ndipo Iye anali—Iye anali akuzungulirazungulira. Ndipo ine ndinamuwona Munthu uyu atayima pansi pa Iye. Iye—Iye si... Tsopano, amenewo si masomphenya pamene iwe umuwona Iye. Izo zimakhala basi zenizeni monga inu mukundiwonera ine. Bwanji, inu mukhoza kumumva Iye akuyenda ndi kuyankhula ndi inu. Ndipo pamene Iye... Chirichonse, izo zimakhala zenizeni basi. Ndipo iwo si masomphenya; Munthuyo wangoyima pamenepo chimodzimodzi basi mmene inu mwachitira. Ndipo liwu Lake ndi chimodzimodzi basi monga langa lingakhalire kapena lanu lingakhalire. Koma masomphenya, chinachake chimene chimabwera patsogolo pako ndipo iwe umachiwona icho, monga choncho. Koma Munthu uyu basi amangobwerapo ndipo amadzaima pamenepo.

²³ Chotero Iye anandiuza ine zimenezo... zimene zikanati zidzachitike. Ndipo Iye ananena kuti a... Mngelo uyu anatsika pansi, ndipo Iye anandiuza ine kuti nditembenuke ndipo ndiyang'ane mbali *iyi*. Ndipo izo zinayang'ana choloza India, tsopano. Ine sindikunena kuti izo zinali ku India, koma kuyandikira kumeneko. Koma iwo anali anthu Achimwenye.

²⁴ Chifukwa, aku Afrika amakhala anthu akuluakulu, ojintcha, olemera-onenepa. Ena a iwo amakhala pafupifupi kutalika mapazi seveni, ndi kulemera, oh, thuu handiredi ndi eyite, mapaundi firii handiredi, ojintcha. Achi Zulu, tsopano, achi Shunghi ndi Basutos, ndi, oh, kuli mitundu yambiri yosiyanasiyana. Kuli mitundu fifitini yosiyanasiyana inakhala pamenepo tsiku limenelo, imene ine ndinkayankhula nayo.

²⁵ Ine ndimakhoza kunena mawu amodzi, monga, “Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu.” Ine ndimakhoza kumwa madzi iwo asanadutse mwa otanthauzira onse. Mmodzi amakhoza kunena kuti... Ndipoponse phokoso!

Ine ndinkaganiza, pamene ndinamva anthu Achipentekoste akuyankhula mmalirime, kuti mwinamwake wina akuyankhula mu mtundu wina wa phokoso ndipo wina nkuyankhula ena, izo zingatheke bwanji mdziko? Koma ine ndikukhulupirira Baibulo limalondola, ndipo ndikudziwa Ilo liri, pamene Ilo linati, “Palibepo phokoso lopanda tanthauzo.” Uko nkulondola.

Ena a iwo amatha kunena, mmodzi wa iwo amapita, “Bluur bluur bluur bluur,” zimenezo zimatanthauza “Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu.” Wina amapita, “Klaki klaki klaki klaki,” ameneyo anali “Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu,”

mu chinenero chake. Chotero ziribe kanthu ndi mtundu wanji wa phokoso, iwo ndi tanthauzo kwinkwake. Uko nkulondola. Ziribe kanthu ndi mtundu wanji wa phokoso umene ilo liri, ilo limatanthauza chinachake kwa winawake kwinkwake. Ndipo pamene Iye anali . . . Iwo amakhoza kupereka zimenezo.

²⁶ Ndipo ine ndinazindikira kuti chakumanzere kwanga, pamene Mngelo ameneyo anatsika ndipo ine ndinawona chowoneka ngati unyinjira pamene, ndipo iwo anali anthu ndi . . . zimawoneka ngati iwo anali ndi—mkwamba mowazungulira iwo, monga *chonchi*, ndipo anali atakulunga ndi kumanga, ngati amukutiramo mwana wakanda, thewera. Ndipo izo zinali. Ndipo ine ndimangotha kuwona patali mmene ine ndimakhoza kuwonera, sichinali china koma anthu. Ndiyeno Mngelo uyu anatembenukira pa kuwala koyenda kwakukulu, ndipo anayamba kusunthira mmbuyo ndi mtsogolo, monga *choncho*. Ndipo ine sindinayambe ndawawonapo anthu ochuluka mmoyo mwanga!

²⁷ Ndipo kenako Mngelo wina uyu anadzabwera pafupi kwenikweni kwa ine, ndipo Iye anati, “Pali firii handiredi sauzande a iwo mu msonkhano umenewo.” Ndipo ine ndinazilemba izo apa. Ndipo inu muzilembe izo pa mtundu wina wa chidutswa cha pepala, monga ine ndinanenera za mnyamata amene anawukitsidwa ku Finland. Inu mulembe zimenezo pa chikutiro cha Baibulo lanu kapena penapake, kuti mu msonkhano uwu (Padzakhala msonkhano. Ndipo inu mudzamva izo kudzera potulukira penapake.) za anthu firii handiredi sauzande akudzabwera ku msonkhano umenewo. Tsopano, mudzawone ngati zimenezo siziri zolondola. Zimenezo zidzakhala kuchulukitsa katatu kukula kwake kwa mmene winawo unali. Mukuona? Anthu firii handiredi sauzande adzabwera pa msonkhanowo. Ndipo ndine wokondwa basi kuti ndipite kumeneko, ine sindikudziwa choti ndichite, pakuti ine ndimakonda kupindulira miyoyo kwa Ambuye wathu.

²⁸ Ndipo pamene, nthawi ina, powona—powona osakhulupirira enieni sarte sauzande akubwera kwa Yesu Khristu mu kuitanira paguwa kumodzi, osakhulupirira enieni sarte sauzande.

²⁹ Tsopano tiyeni tipite ku phunziro lathu mwamsangamsanga. Dzulo ife tinaphunzira za njomba ya ziwanda. Ine ndakhala ndikuganzira lero, pamene Mulungu akuchita. Inu simukudziwa kuti ndi ufulu wotani kuti uchokemo. Tsopano, ine sindine mphunzitsi. Ine ndiri kutali kuti ndingakhale—wolifotokoza Baibulo. Ndipo ine ndine . . . Maphunziro anga ndi operewera a kalasi ya seveni. Chotero ndizo . . . Ndipo, izo, ine ndinasiya sukulu pafupifupi zaka twente-faivi zapitazo, chotero limenelo ndi kale kwambiri. Ndipo ine ndiribe maphunziro ochuluka, koma zonse zimene ine ndimadziwa ndi chimene ine ndimalandira kudzera mwa kuzodza. Ndipo ngati kuzodza

kumeneko sikufanana ndi Baibulo, ndiye iko ndi kolakwika. Mukuona? Iko kukuyenera kukhala Baibulo. Ziribe kanthu kuti kuzodzako ndi kotani, iko kukuyenera kubwera. . . *Apa* pali maziko a Mulungu. Palibe maziko ena amene anaikidwa koma Awa. Ndipo chimene Ili liri, ngati chimene ine ndinganene chingakhale chosemphana ndi Ili, inu mulole mawu anga akhale abodza, chifukwa Ichi ndi Choonadi. Mukuona? Mukuona? Ndipo ngati mngelo atakuuzani inu chinachake chimene chingakhale chosiyana ndi Ili, Paulo anati, “Musiyeni iye akhale kwa inu themberero,” ngakhale mngelo wa Kuwala. Tsopano, pali zinthu zambiri zazikulu. Ine basi. . . basi. . . Ine ndinasankha masiku awiri, chifukwa kuti nditengere phunziro ili kwa anthu, limenelo linali dzulo ndi lero, misonkhano ya masana.

³⁰ Tsopano, chifukwa chimene ine ndinachitira izi, ndi kuti ndizipatse ndekha kuyesera pang’ono kuti ndiwone ngati Mulungu angandithandize ine. Pali chinachake pa mtima panga. Ndipo ichi ndi, kuti, Uthenga waukulu uwu ukatha, ndipo Mulungu Iyemwini atatha kutsimikizira chimene ine ndanena kuti ndi Choonadi, mu Mawu Ake; mwa Mawu Ake, poyamba, ndipo kenako kudzera mu zizindikiro ndi zodabwitsa. Tsopano, ine ndikuganiza, ndi Choonadi cha Uthenga ku Mpingo, ine ndiri ndi udindo, kwa Mulungu, kuti ndibweretse izi kwa Mpingo. Uko nkulondola. Iwo ndi osweka kwambiri, mu mabungwe osiyanasiyana ambiri ndi magawo achipembedzo a iwo, mpaka izo ndi zolakwika. Ndife tonse ana a Mulungu pamene ife tibadwa mwatsopano, Izo, mwaona. Ndipo choonadi cha chinthucho ndi chakuti Mulungu akufuna ife tidziwe zimenezo, kuti ndife ana Ake.

³¹ Tsopano, kumbukirani, kachisi wa Solomoni anadulidwa, kuzungulira dziko lonse. Ndipo apa panabwera mwala umodzi wopotokera mbali *iyi*, ndipo mwala umodzi wopotokera mbali *iyi*, ndipo wina wodulidwa mwanjira *iyi*, ndipo wodulidwa mwanjira *iyi*, koma, pamene iyo inabwera pamodzi, panalibe kulira kwa macheka, ngakhale phokoso la nyundo, uliwonse umapita moyenera pamalo pake. Mulungu anali Mlangizi wa izo.

³² Mulungu ali nawo mpingo wotchedwa Assemblies, ndipo wina church of God, ndipo wina *ichi*, ndipo wina *icho*. Ndipo, koma pamene iwo onse abwera pamodzi, iwo amadzakhala gulu lalikulu limodzi la chikondi cha pa abale, ndipo Mulungu adzaika, adzasonkhanitsa Mpingo umenewo pamodzi ndi kudzawutengera Iwo mu mlengalenga.

³³ Chithunzi chotchuka chirichonse, icho chisanakolekedwe mnyumba ya zaluso, icho chimayenera kukolekedwa, nkudutsa mu nyumba ya otsutsa, poyamba. Munthu amene anajambula. . .? . . ., kapena, mundikhulukire ine, ine sindingatchule dzina lake, anajambula Mgonero Womaliza, mulimonse, izo zinamutengera iye nthawi ya moyo wake.

Iye anajambula chithunzi chimenecho. Izo zinali pafupifupi zaka twente, kapena zaka teni, ine ndikukhulupirira, pakati pojambula Khristu ndi Yudasi. Ndipo kodi inu munazindikira, mu chithunzi chotchuka chimenecho, kuti munthu yemweyo anawoneka ngati Khristu, zaka teni mtsogolo anadzawonekera ngati Yudasi? Uko nkulondola. Iye anatero. Zaka teni za tchimo, kuchokera kokhala woyimba wa opera wamkulu, kudzatenga malo a Khristu, anadzabwera pamalo a Yudasi. Inu simukusowa kutenga zaka teni. Izo zimatengera maminiti teni, zidzachita chinthu chomwecho kwa inu. Izo zidzasintha khalidwe lanu, mu tchimo. Koma, mulimonse, chithunzi chimenecho chinadutsa mwa otsutsa onse.

³⁴ Ndipo ndicho chimene ine ndimaganiza za Mpingo wa Mulungu, gulu limene litanidwa. Chabwino, ine sindikutanthauza izi kudzera mwa chonyoza chirichonse. Ine ndayendapo pa nyanja zazikulu seveni, ndipo ine ndiri pa ulendo wanga wachitatu kuzungulira dziko, ndipo anthu amati, “Woyera-wodzigudubuza! Woyera-wodzigudubuza!” Ndipo ine ndafufuza pa dziko lapansi, ndipo sindinayambe ndamupezapo woyera wodzigudubuza. Limenero ndi dzina limene mdierekezi waliika pa anthu. Ndizo zonse. Palibepo chinthu chotero ngati woyera wodzigudubuza. Ndipo ine ndiri ndi chiwerengero cha mipingo sikisi handiredi ndi sikisite eyiti yosiyanasiyana imene ilipo, ndipo yopangidwa bungwe mu dziko, palibepo umodzi wa iwo umene umatchedwa Oyera Odzigudubuza. Ndipo zimenezo ndi zochokera ku boma. Palibepo mpingo umodzi wa Odzigudubuza Woyera umene ine ndimawuziwa. Chotero, ndi chinachake chimene mdierekezi anachitchula. Koma, tsopano, mu zonsezi, zinthu zonsezi, Mulungu anajambula chithunzi. Ndipo nthawiina mipingo yakale yaying’ono iyi inali kunja kuno, ena a inu . . .

³⁵ Ine ndimawawona amuna a mmutu mwa imvi awa. Mnyamata wanga, dzulo; Ine ndinali mchipinda, ndikuwerenga, ndipo mtumiki anabwera ndipo anati, “Ndikufuna ndigwirane chanza ndi bambo ako.” Ndithudi, mnyamata wanga waleredwa ndi M’bale Baxter ndi iwo, amene basi, “Ayi,” ndi zimenezo, mwamsanga. Ine sindimazikonda izo. Mukuona? Ziribe kanthu ngati ine. . . Ndithudi, ine sindingakhale wantchito wa munthu ndi Mulungu, nanenso. Koma ine ndikuganiza ndimakonda kugwirana chanza ndi abale anga. Ine ndimakonda kuchita zimenezo. Pali chinachake cha izo, ine ndimakonda kugwirana chanza dzanja la—la mtumiki. Osati mtumiki yekha, koma mwana aliyense wa Mulungu, ine ndimakonda kuchita zimenezo. Ine sindinadziwe za izo mpaka mkazi wanga atadzandiuza ine mtsogolo mwake. Chabwino, ngati iye akanamuza mtumiki ameneyo, “Miniti chabe, iye ali kumbuyo uko mu pemphero, ndipo—ndipo ine ndiwona chimene iye ati anene.” Chabwino, izo, izo zikanakhala zabwino. Chotero ine

ndinamukonza iye pang’ono pa izo, kuti asamachite zimenezo. Mukuona?

³⁶ Ndipo chotero izo nzoona, iwe sungamangokhala kunjani nthawi zonse, monga m’bale ananenera kanthawi kapitako. Ngati iwe utero, ndiye usiku ine—ine ndimatopa, inu mwaona. Anthu akayamba kuyankhula, ndipo aliyense mwinamwake ali ndi nthenda, ndipo akayamba kuyankhula za zimenezo, mwamsanga, pamakhala Mngelo wa Ambuye pomwe apo woti anene za izo.

³⁷ Pali winawake wakhala, akundiyan’ana ine tsopano, akudziwa kuti izo ndi zooni, kuchokera maminiti pang’ono apitawo, kapena pafupifupi ora ndi theka lapitalo. Dona wakhala apa, amene samadziwa chimene izo zinali, kuti Mngelo wa Ambuye anayankhulana naye usiku wina ndipo anamuuzi iye chinachake, ndipo iye samamvetsa izo. Koma lero izo zinachitika, chotero iye akudziwa tsopano chimene izo zimatanthauza pamene Iye amayankhula ndi iye. Ndipo momwe, atayima pamenepo akuyankhula ndi iye, Mngelo wa Ambuye anapita molunjika kumbuyo uko ndipo anamuuzi iye chimene vuto lake linali, ndi chimene zonsezo zinali, ndi—ndi chimene iye ankachiganizira, ndipo mmodzi wa okondedwa ake, ndipo mmene Mulungu anayankhulira ndi kunena kuti Iye anatsimikizira izo, ndi chimene chikanati chidzachitike. Chotero izo ndizo ndendende mmene izo ziti zidzakhali. Mukuona? Mulungu anali atanena choncho.

³⁸ Chabwino, tsopano, nanga bwanji nthawi zochepa zimene. . . Kenako, ndipo masomphenya aliwonse amangokufooketsa iwe mochuluka chomwecho, mwaona. Ndipo chinthu choyambirira iwe ukudziwa, pamene iwe ufika ku tchalitchi usiku, iwe umangokhala utathekeratu kwathunthu mpaka iwe sumadziwa nkomwe choti uchite. Ndipo inu muzindipempherera ine tsopano, mwaona, chifukwa izo zimachoka mu msonkhano umodzi kupita kwa wina, kupita kwa wina. Uwu unali msonkhano wokhawo, izo zikanakhala zosiyana, ngati ine ndikanati ndikupita kwathu tsopano ndipo ndinali woti sindichita kalikonse kwa miyezi ingapo, kupita uko ndi kukatenga mbedza yanga ndi kumapita kowedza. Koma ine ndimayenera kupita kuchoka ku msonkhano umodzi kupita kwa wina, kuchoka ku umodzi pomwepo kupita kwa wina, inu mwaona. Izo ndi zimene zimachititsa izo.

³⁹ Ndipo inu nonse mupemphere, anthu inu kumbuyo uko mwa omvetsera. Iwo anandiuzi ine usiku wathawu kuti ine—kuti ine ndimayankhula kwa munthu winawake, ndipo munthuyo sanayankhe foniyo. Tsopano, zimenezo ndi zowopsya kwambiri, inu mwaona. Pamene iwo ananena izo. . . Chabwino, nthawizina nyali zizi sizimawala, pali dontho lakuda pakati pamenepo.

⁴⁰ Ndipo ine ndimamuyang'ana Mngelo wa Ambuye pamene Iye waima apa, ine ndimakhoza kumverera izo. Kenako ine ndimamumva Iye akuchoka kwa ine, ndipo ine ndimapenyetsetsa, Iye amandichokera ine ndipo Iye amapita penapake ndi kukaima pamenepo pang'ono, ndipo ine ndimatha kumuwona Iye. Ndipo Iye amathwanima ndipo pamenepo pamabwera masomphenya. Kenako ine ndimawona masomphenya. Ine ndimawona mtundu wa munthu wooneka bwanji amene ali mozungulira pamenepo. Ine ndikamupeza munthuyo, kenako ndimayankhula. Ndi zimene zimachitika. Ndi zimene zimachitika. Iwe sumayenera kumuuza aliyense zimenezo, koma ndizo—ndi zimene zimachitika, inu mwaona. Zonsezo zimakhala mu dera lauzimu.

⁴¹ Ndiye ngati munthu ameneyo sayankhira, izo zimakhala ngati kuwenga Baibulo apa ndi kumati, “Palibe kalikonse kwa Ilo,” nkuchoka kwa Ilo. Mukuona? Chotero izo zimakhala zoyipa kwambiri. Chotero muzikhala tcheru, muzimvetsera, muzipenyetsetsa. Iye akayankhula, muziyankha. Mwaona, muzingokhala okonzeka kuyankha nthawi ziliyonse.

⁴² Ndipo chotero mkazi wanga, ndi M'bale Beeler ndi ambiri a iwo, mmawa uno, amandiuza ine za izo, kuti amayitana munthu zokhudza m'bale wake, kwinkwake, amene anali ndi chinachake chovuta ndi iye, ndi zina zotero. Ndipo munthuyo sanayankhire ku kuitanako, chotero izo sizingathandizidwe. Izo zimakhala pakati pa Mulungu ndi munthuyo. Masomphenyawo anandichokera ine. Kenako ine sindinadzawapezenso iwo, chifukwa iye sanayankhire. Chotero, mudzipenyetsetsa, mudzikhala tcheru.

⁴³ Tsopano kutenga phunziro ili la *Phunziro La Ziwanda* ndi kuyankhula za ziwanda. Tsopano, anthu, pamene iwe unena kuti “chiwanda,” mwamsanga iwo amayamba kuganizira, “Oh, kutengeka kwinkwake kapena chinachake!” Koma ziwanda ndi zenizeni basi monga ngati Angelo. Izo ndi zenizeni basi.

⁴⁴ Ndipo mdierekezi ndi weniweni basi mdierekezi, monga Yesu Khristu aliri Mwana wa Mulungu. Iye ndi mdierekezi! Kumwamba ndi kwenikweni basi. Ndipo ngati kulibeko chinthu chotchedwa gehena, kulibeko chinthu chotchedwa Kumwamba. Ndipo ngati kulibe odalitsika Amuyaya . . . chilango Chamuyaya, kani, kulibeko odalitsika Amuyaya. Ngati kulibeko usana, kulibeko usiku. Mukuona? Koma motsimikiza basi mmene kuliri usana, usiku ulipo. Monga—motsimikiza basi mmene ulipo—motsimikiza basi monga Mkhristu alipo, pakuyenera kukhala wachinyengo. Motsimikiza basi monga alipo winawake weniweni wochokera kwa Mulungu, alipo winawake woti anyengezere izo. Mukuona? Izo ndi ndendende chotsutsa ndi chovomereza, chakuda ndi choyera, kudutsa mmoyo pa chirichonse, choona ndi chabodza paliponse. Ndipo ulipo uthenga wabodza, ulipo Uthenga woona. Uli Ubatizo woona,

ulipo ubatizo wabodza. Pali wodzipangitsa kukhulupirira, ndipo pali weniweni. Pali dolla ya Amerika yeniyeni, palinso dolla ya Amerika yabodza. Alipo Mkhristu weniweni, alipo wonyenga weniweni, mwaona, amene akungonyengezera. Chotero inu mumazipeza zimenezo, chotero izo zimangoyendera limodzi. Tsopano, ife sitingathe kuzilekanitsa izo. Mulungu amailola mvula igwe.

⁴⁵ Mulole Iye andilole ine ndiyankhule apa pang’ono pokha. Ndi alaliki angati amene ali pano? Kwezani mmwamba manja anu. Kuzungulira konsekonse, alaliki, tiyeni tiwone manja anu. Chabwino, Mulungu akudalitseni inu, abale. Tsopano, tsopano, inu musatenge ichi ngati chiphunzitsa tsopano, koma, basi tisanafike ku phunziro lofunikira ili, Ine ndikuuzani inu chiyani. Ndi anthu angati Achipentekoste amene ali pano? Kwezani mmwamba manja anu, nonse kuzungulira paliponse. Chabwino, ndinu nonse Achipentekoste. Chabwino. Ndi kuuzani inu chimene ine ndinali nacho pamene ine ndinabwera koyamba mu gawo lanu, udindo.

Ine ndinali kumtunda komwe kuno mu Indiana, ku malo ena ake otchedwa Mishawaka. Gulu loyambirira la anthu Achipentekoste limene ine ndinayamba ndaliwonapo, ili linkatchedwa pe—Pentecostal Assemblies of Jesus Christ, Ine ndikukhulupirira, kapena chinachake chonga zimenezo, gulu lodabwitsa la anthu. Tsopano iwo apanga bungwe pamodzi ndipo amawatcha iwo United Pentecost. Iwo anachoka kwa ena onsewo, chifukwa cha nkhani ya ubatizo wa mmadzi. Zimenezo sizimawapanga iwo kukhala achinyengo nkomwe. Alipo Mkhristu weniweni, wa Mzimu Woyera weniweni, wobadwa mwatsopano mmaudindo awo. Ndipo Mulungu anawapatsa iwo Mzimu Woyera pobatizidwa mu “Dzina la Yesu,” ndipo anawapatsa enawo ubatizo wa Mzimu Woyera, pobatizidwa mwa “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Chotero, “Mulungu anawapatsa iwo Mzimu Woyera, amene amamumvera Iye,” chotero ndi ndani—ndi ndani, ndi ndani anamumvera Iye? Ndi zimenezotu.

⁴⁶ Ngati inu mungangoiwala, ndipo iwo amene akufuna kukhala njira imodzi, aloleni iwo akhale, ndipo inu muzipitirira ndi kukhala abale. Ndizo zonse. Musati. . . Chimene chinachita izo, chinali kuwaphwasula iwo, kuchokapo. Mukuona? Chiyani? Kunali kuphwasula, kung’amba, kupasula ubale, kukhazikitsa ndi kudzilekanitsa nokha. Ayi, bwana, ife sitinalekane, ndife amodzi. Uko nkulondola.

⁴⁷ Koma pamene ine ndinali nditaima pamenepo, ine ndinali kuwawona anthu amenewo. Tsopano, ine, nditangochokera ku mpingo waung’ono wakale wa Southern Baptist, bwanji, Ine ndimatha kuwaona anthu amenewo, ine ndinalowa mmenemo ndipo iwo anali akuwomba manja awo, akufuula, “Mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo, wokondwa kunena ndine mmodzi wa iwo!”

48 Ine ndinaganiza, “Mai! Psyii!” Chinthu choyamba inu mukudziwa, apa panabwera winawake akudutsa pamenepe, akuvina molimba mmene iye akanathera. “Tuh-tuh-tuh-tuh-tuh,” ine ndinaganiza, “makhalidwe a mtundu wanji a mpingo! Ine sindinayambe ndamvapo zinthu zonga zimenezo.” Ine ndinapitirira kumawayankha iwo, pozungulira. Ndinadabwa, “Chabwino, kodi vuto ndi chiyani mdziko ndi anthu amenewo?”

49 Tsopano, inu munandimvapo ine ndikunena mbiri ya moyo wanga, pamene ine ndinafika pa msonkhano umenewo uko. Koma ichi ndi chinthu chimodzi chimene ine sindinayambe ndachinenapo, sindinachinenepo mmbuyomo, pagulu. Chotero iwo . . . Tsopano, ngati inu mukufuna kuzifufuta izo pa chojambulira chanu, bwanji, inu mukhoza kutero. Chabwino. Tsopano, mu ichi ine ndinkawona, ndipo tsopano ine ndinaganiza, “Chabwino, anthu amenewo ndi anthu okondwetsetsa amene ine ndinawawonapo mmoyo mwanga.” Iwo sankachita manyazi ndi chipembedzo chawo. Iye a Baptist timangochita manyazi pang’ono, apo ndi apo, inu mukudziwa. Mukuona? Ndipo pamene iwo anayamba kupemphera, inu mukudziwa, iwo amakhala kuseri kwa chokupiza mphepo, inu mukudziwa. Ndipo—ndipo, koma ife . . . Koma anthu amenewo sanali, m’bale, iwo—iwo anali ndi chipembedzo mkati monse, kunja, ndi paliponse powazungulira iwo.

50 Chabwino, ine ndikukumbukira usiku umenewo pamene ine ndinadzafika pa nsanja. Ndinati, “Alaliki onse pa nsanja.” Iwo unali msonkhano waukulu. Iwo ankayenera kukhala nawo kumtunda kuno Kumpoto, pa chifukwa cha—pa chifukwa cha vuto la achikuda, lamulo la Jim Crow wa Kummwera. Chotero iwo onse anakumana kumeneko kuchokera kulikonse. Chotero, ine ndinali nditakhala kumeneko. Ndipo iye anati . . . Chabwino, tsopano pali . . . Ndinawamva alaliki onse kudutsa tsiku limenelo ndi usiku umenewo. Iwo anati mlaliki wina wachikale, iye anali bambo wokalamba wachikuda anadzuka, basi wa tsitsi pang’ono pa mutu pake, monga *choncho*, atavala chikhotho cha mlaliki chakale chachikulu chachitali, inu mukudziwa, kolala ya veliveti, ndi nyengo yotentha. Munthu wosauka wokalamayo anatuluka pamenepe monga *chonchi*. Iye anati, “Ana anga okonedwa,” iye anati, “Ine ndikufuna ndikuuzeni inu,” anayamba kuchitira umboni. Ine ndinali wamng’ono kwambiri amene ndinakhala pa nsanja. Chotero ndiye iye anati, “Ine ndikukuuzani inu!” Iye anatenga phunziro lake kuchokera mu Yobu, “Iwe unali kuti pamene Ine ndinkaika maziko a dziko lapansi? Ndiuze Ine pamene iwo anamangiriridwapo.”

51 Alaliki ena onsewa anali akulalikira za Khristu, mwa kachitidwe kozolowereka. Ine ndinawamvetsera iwo, kusangalala nawo. Koma osati mnyamata wokalamba ameneyo! Iye anabwerera mmbuyo pafupifupi zaka teni sauzande dziko lisanayambe konse. Iye anapita Mmiyamba ndipo anatsika

mlengalenga, zimene zinkachitika. Zimene iwo ankalalikirira, zikupitirira, tsiku ndi tsiku; iye anali akulalikirira pa zimene zinkachitika Kumwamba. Iye anamubweretsanso Khristu pa utawaleza wopingasa, kubwerera mmbuyo uko kwinkakwaka ku Umuyaya. Bwanji, iye sanalalikirira kwa pafupifupi maminiti faivi mpaka bambo wokalamba uyo, Chinachake chinamugwira iye. Iye analumpha mmalere ndipo anamenyetsa zidendene zake pamodzi, ndipo anafuula, “Wuuphii!” Iye anali ndi malo monga amene ine ndiri nawo pano. Iye anati, “Inu mulibe malo okwanira kuti ine ndilalikirira,” ndipo iye anachokapo.

⁵² Chabwino, ine ndinaganiza, “Ngati icho chingachite zimenezo kwa mwamuna wa pafupifupi usinkhu wa zaka eyite zakubadwa, icho chingachite chiyani kwa ine? Ndicho chimene ine ndikuchifuna. Ndicho chimene ine ndikuchifuna.”

⁵³ Koma chimene chinandikhudza ine chinali ichi. Tsopano, ife tikukamba za ziwanda tsopano. Chimene chinandikhudza ine, ine ndinawona amuna awiri. Mmodzi anakhala mbali imodzi, ndipo wina mbali yinayo. Ndipo pamene Mzimu ukati wagwa, amuna amenewo ankadzuka ndi kuyankhula mmalirime ndi kufuula, ndipo pakamwa thovu loyera. Ndipo ine ndinaganiza, “Oh, mai, ngati ine nditangokhala ndi zimenezo!” Mukuona? “Nzodabwitsa bwanji! Oh, ndizo. . . ine ndikungozikonda zimenezo!” Chabwino, ine ndinapita panja mmunda wa chimanga. Ndipo ine ndinakuuzani inu mbiri ya moyo wanga. Inu mumaiwerenga iyo mu bukhu. Ine ndinagona usiku wonse. Ndipo ine ndinabwerera mmawa wotsatira, chotero ine ndinaganiza ine ndingoyesa. Ine ndiri nayo njira yochitira zinthu imene palibe amene amaidziwa koma Mulungu ndi ine. Chotero, izo, ine ndimatenga fanizo ndipo ndimapita kukakumana ndi mzimu wa munthuyo. Inu mumaziwona izo pomwe pano pa nsanja. Mukuona? Ndipo chotero ndiye ine ndinayamba kuyankhula ndi mmodzi wa amuna amenewo. Ine ndinawawona iwo, iwo anakhala moyandikana pamodzi, ndipo iwo anangogwirana manja ndi kumavina ndi kumafuula. Ine ndinaganiza, “Oh, mai, izo zikumveka zenizeni kwa ine!”

⁵⁴ Ndipo ine ndinagwira limodzi la manja ake. Ine ndinati, “Inu muli bwanji, bwana?”

⁵⁵ Iye anati, “Inu muli bwanji.” Mwamuna wabwino kwambiri, wokhala ngati njonda. Iye anati. . .

Ine ndinati, “Kodi ndinu mtumiki?”

Iye anati, “Ayi, bwana. Ine ndangokhala membala wamba.”

⁵⁶ Ndipo ine ndinayamba kuyankhulana naye iye pang’ono kuchitira kuti ndigwire mzimu wake. Mukuona? Iye samadziwa zimenezo. Panalibe ankadziwa. Ine sindinanene kanthu za izo. Zaka mtsogolo, ine ndisanatchule izo. Chotero iwo. . . Koma pamene ine ndinadzapeza, izo zinali zooni, mwangwiro basi, mwamuna Wachikhristu! Mwamuna ameneyo mwamtheradi

anali woyera wa Mulungu. Ine ndinaganiza, “M’bale, izo ndi zabwino.”

⁵⁷ Koma gawo lachirendo, pamene ine ndinadzamugwira mwamuna winayo, izo zinali zosiyana. Iye ankakhala ndi mkazi amene sanali mkazi wake nkomwe. Uko nkulondola. Ndipo ine ndinawona izo zikukokera kwa iye, masomphenya. Ine ndinaganiza, “Oh, mai, izo sizingakhale chomwecho.” Ndipo mwamunayo . . . ine ndinaganiza, “Tsopano, tsopano, mzimu uwu umene uli pakati pa anthu amenewo ndi wolakwika. Ndizo zonse zimene ziripo kwa izo.”

⁵⁸ Chotero usiku umenewo pamene . . . ndinapita ku msonkhano, ndipo madalitso amagwa, ine ndinali kupemphera kwa Mulungu, ndipo Mzimu Woyera, Mngelo wa Ambuye umaperekeru umboni kuti iwo unali Mzimu Woyera. Ndipo Mzimu womwewo unali ukugwa pa mwamuna *uyu* umagwera pa mwamuna *uyo*. Ndipo Mzimu ukagwa, awiriwo ankadzuka, ndipo awiri onse amafuula ndi kukuwa ndi kumutamanda Ambuye, ndi kuyankhula malirime ndi kumavina. Ine ndinati, “Ine—ine—ine sindikuzimvetsa zimenezo, Ambuye. A . . . ine sindikuziwona izo mu Baibulo, pamene izo zingakhale zooni.” Tsopano ine ndinati, “Mwinamwake ine ndanyengedwa.” Mukuona? Ine ndinati . . . Tsopano, apa, ine—ine sindi . . . ndine—ndine wokhazikika mosamalitsa mu Baibulo. Izo zikuyenera kukhala Ichi. Mukuona? Ine ndinati, “Ambuye, Inu mukudziwa mmene ziliri ndi ine, ndipo ine—ine ndikuyenera kuziwona izo mu Mawu Anu. Ndipo ine—ine sindikuzimvetsa. Pamene Mzimu Woyera ukugwera pa mwamuna *uyu*, Mzimu Woyera ukugwera pa mwamuna *uyo*, ndipo mmodzi wa iwo ndi woyera ndipo winayo ndi wachinyengo. Ndipo ine ndikudziwa ziri chomwecho.” Ine ndikuzidziwa zimenezo. Popanda . . . ine ndikanamutengera mwamunayo panja ndi kukatsimikizira izo kwa iye, kapena kumuitanira iye panja pomwe apo ndi kumuza iye za izo.

⁵⁹ Monga ine ndikanachitira ndi mwamuna uyo anakhala apa usiku wapitawu, sanali kanthu koma—a wonyenga, ngati pakanakhala mmodzi atakhala pamenepo. Ndipo ine ndinkayenera kuchitchula icho, koma iye akanadzuka ndi kuyamba zokangana. Chotero ine ndinangozisiya izo zipipita, pa chifukwa cha msonkhano, koma ine ndinamudziwa iye. Inde, bwana.

Pali wina, awiri a iwo, anakhala kumbuyo uko, usiku wina, a mpingo wina komwe kuno mu mzinda. Otsutsa enieni! Ine ndinawawona iwo. Koma, ngati iwe ungatero, izo zimayambitsa mavuto. Ine ndachitapo izo nthawi zambiri. Ine ndimangowasiya iwo okha, mwaona. Izo ziri bwino. Mulungu amadziwa, Iye ndi Woweruza. Mudzawalole iwo azandiitane ine nthawi ina, ndiyeno inu mudzawona chinachake chikuchitika, inu mwaona, mudzamulole iye.

Monga chiwanda, ine sindinachiitane chiwanda. Iye anangobwera kwa ine ndi kudzanditsutsa ine. Pamenepo ndi pamene Mulungu anapita kukagwira ntchito, mwaona, uko nkulondola, ndipo inu munawona zimene zinachitika. Chabwino. Koma ine ndinangozilola izo kuti zipite. Zinapangitsa msonkhano kukhala wovuta, chifukwa mzimu umenewo umayenda pa ine nthawi yonse, mwaona. Ndipo chotero ine ndimangopitirira.

⁶⁰ Koma tsopano, amuna awa, ine sindimazimvetisa izo. Ndipo panali zaka ziwiri mtsogolo mwake, kapena zitatu, pamene ine ndinali uko ku Green’s Mill, Indiana, kuno, ku scout reservation. Ine ndinabwerera mu mphanga yakale kumene ndimapita kukapemphera. Ndipo kumbuyo uko, ine ndinati, “Ambuye, ine sindikumvetisa chimene chinachitikira gulu la anthu amenewo. Anthu abwino kwambiri amene ine ndinayamba ndakumanapo nawo mmoyo mwanga, ndipo ine—ine sindikumvetisa mmene umenewo ungakhalire mzimu wolakwika. Pamene izo ndi... ngati ndiye... Inu mukudziwa ungwiro wa mtima wanga. Inu mukudziwa mmene ine ndimakukonderani Inu ndi mmene ndakutumikirirani Inu. Ndi Mzimu womwewo umene uli pano, ndi ine, unali pa anthu amenewo. Ndipo apa Iwo unali pa mnyamata ameneyo, pamenepo, basi chimodzimodzi.” Chotero ine sindimamvetisa.

⁶¹ Ndipo Ambuye anatsika pansu mu chifundo Chake ndipo anadzandiwonetsa ine. Apa ndi pamene icho chinali. Ichu chikuyenera kukhala cha Mwamalemba, poyamba. Iye anati “Tenga Baibulo lako.” Ndipo ine ndinatenga Baibulo langa. Ine ndikuganiza ndinalinyamula Baibulo limenelo kwa maminiti teni popanda aliynse... Mawu aliwonse akubwera. Ine ndinadikirira kwa mphindi pang’ono. Ine ndinamumva Iye akunena kenanso, “Tsegula ku Ahebri 6 ndipo uyambe kuwenga.” Ndipo ine ndinatero. Ndipo pamene zinafika pamenepo, pamene Ilo linati, “Mvula imabwera mowirikiza pa nthaka kuti ithirire iyo ndi kuikonzekeretsa iyo, kuikona iyo kwa chimene iyo... koma minga ndi nthula, zimene zimayandikira ku kukanidwa, zimene mapeto ake ndi kukawotchedwa.” Ndipo ine ndinachigwira icho pomwepo.

Ine ndinaganiza, “Ndi zimenezo apo. Mathokozi apite kwa Mulungu! Ndi zimenezo apo.” Mukuona?

⁶² Tsopano, Yesu anati, “Wofesa anapita kukafesa mbewu,” sichoncho Iye? Tsopano, ndinu nonse Akhristu pano. Aliynse anakweza mmwamba manja awo, mulimonse, Achipentekoste, Akhristu obadwa mwatsopano. Chabwino. Iwo... Ndipo Iye anati, “Wofesa anapita, kukafesa mbewu. Ndipo pamene iye anagona...” Mpumulo wake, imfa, pakati. Mukuona? “Ndipo pamene iye anali kugona, mdani anadzabwera ndipo anafesa namsongole mmunda mmenemo.” Kodi namsongole ndi chiyani? Maudzu, minga ndi zinthu. Tsopano, “Ndipo pamene

wosamalirayo (mlaliki) anawona namsongole uyu akukula, anati, 'Ndiloleni ine ndipite ndikamuzule iye. Iye anati, 'Ayi, ayi. Iwe uzulanso tirigu. Zilole ziwiri zonsezo zikulire limodzi.'"

⁶³ Pali munda wa tirigu kunja kuno. Pali zoyanga, chisoso, udzu womata, china chirichonse mmenemo. Nkulondola uko? Koma, tsopano, mmenemo muli tirigu. Tsopano, mvula imabwera mowirikiza pa dziko lapansi, kuti idzathirire iwo. Tsopano, kodi mvulayo ndi yachiyani? Osati kudzathirira chisoso. Tsopano penyani ndipo mukhale tcheru. Osati kudzathirira zoyanga. Mvula imatumizidwa chifukwa cha tirigu, koma chisoso ndi udzu zimakhala ndi ludzu basi monga momwe tirigu amakhalira. Ndipo mvula yomweyo imene imagwera pa tirigu imagwera pa udzu. Ndipo udzu waung'ono wakale umayima pomwepo utadzuka monga choncho, ndipo wokondwa ndi kumasangalala, chimodzimodzi basi monga tirigu wamng'ono angadzukire ndi kudziimitsa yekha.

⁶⁴ "Koma ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo." Ndi zimenezotu. Mukuona? Tsopano, Mzimu Woyera womwewo ukhoza kumudalitsa wachinyengo. Zimenezo zakugwetsani ena a inu a chi Arminian, koma icho ndi Choonadi. Icho ndi Choonadi. Munaphunzitsidwa za chiyero, chimene ine ndimakhulupirira mu chiyero, nanenso. Koma Mzimu womwewo, mvula imagwera pa olungama ndi osalungama, koma ndi zipatso zawo inu mudzawadziwa iwo.

⁶⁵ Ngati ine ndingayang'ane apa ndi kupita kukatenga tirigu, ine ndikatenga tirigu, koma udzu wonse ndiwomangidwa. Ndipo izo zikukhala moyo chifukwa cha mvula yomweyo imene inagwera pa tirigu. Ndipo mvula sinatumizidwe chifukwa cha udzu, iyo inatumizidwa chifukwa cha Tirigu. Koma mvula pokhala mmundamo, tirigu pokhala. . . udzu pokhala mmunda wa tiriguwo, unangopeza phindu lochuluka chimodzimodzi kuchokera ku mvula monga zina zonsezo zinkachitira. Ndipo mvula yomweyo imene inapangitsa tirigu kukhala moyo, inapangitsa udzu kukhala moyo.

⁶⁶ Zinthu zonse mu zachirengedwe zimayimira zauzimu, pamene ife tikuphunzitsa. Ndi zimenezotu, phunziro la ziwanda, ziwanda zikunyengezera Chikhristu, komabe, ndi mdalitso. Izo si mkaka wosungunula, abale, ngati inu mungatenge izo. Mukuona? Mukuona? Tsopano, icho—icho ndi Choonadi.

⁶⁷ Chotero, sindine wopulumutsidwa lero chifukwa chakuti ndikhoza kufuula. Ndine wopulumutsidwa osati chifukwa choti ndikumverera ngati ndapulumutsidwa. Ndine wopulumutsidwa chifukwa chakuti ndinakumana ndi zoyenerenza za Mulungu za Baibulo ili. Yesu anati, "Iye amene amva Mawu Anga ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha, ndipo sadzafika ku chiwonongeko, koma wachoka ku imfa wapita ku Moyo." Ine ndikukhulupirira zimenezo. Uko

nkulondola. Ndipo pa mfundo zimenezo ine ndapulumsidwa, chifukwa Mulungu anatero.

⁶⁸ Ngati iye akanandiuza ine inu mwapulumutsidwa chifukwa winawake anati, “Mphepo ya nkokomo inandiwomba ine pa nkhope,” izo nzodabwitsa, koma ine ndikufuna ndidziwe kumene mphepo ya nkokomo imeneyo inachokera iyo isanadzandiwombe ine pa nkhope yanga, mwaona. Tsopano, inu mukakhala moyo wa mtundu wanji mphepo ya nkokomo imeneyo itatha kukuwombani inu? Mukuona? Mwaona, ndi mwa chipatso chanu inu mumadziwika. Chotero, ziwanda zikhoza kugwira ntchito pakati pa Akhristu kumene. Inu mukukhulupirira zimenezo? Tamuonani Paulo, Paulo anati. . .

⁶⁹ Tsopano apa ndi pamene a Mvula ya Tsiku la Masika. . . Ngati mulipo ena a inu pano, mundikhulukire ine ngati ndikunena chirichonse motsutsana ndi inu. Ine sindinganene zochulukana zotsutsana ndi inu kuposa mmene ndingachitire ndi a Assemblies, kapena aliyense, a Baptist, kapena wina aliyense. Ndicho Choonadi chake ndi chimene chiri Choonadi. Chimene inu mwaphonya, ndi ichi: inu mukupanga aneneri kuchokera mwa amuna amenewo ndi zinthu zimene si aneneri. Aneneri “samachita kuikidwa manja” ndi kutumidwa. Aneneri amachita kubadwa. Mukuona? Mu Baibulo, muli *mphatso* ya uneneri. Pamenepo ndi pamene inu munalakwitsira, pakati pa *mphatso* ya uneneri ndi mneneri. *Mphatso*. . .

⁷⁰ “Mulungu, mu nthawi zamakedzana ndi mmachitidwe osiyanasiyana ankayankhula kwa makolo kudzera mwa aneneri, mu masiku otsiriza ano kudzera mwa Mwana Wake, Khristu Yesu.” Ndipo Thupi la Khristu liri ndi *mphatso* zauzimu naini zikugwira ntchito mmenemo. Ndipo iyo ikhoza kukhala pa mkazi *uyu* usikuuno, uneneri, ikhoza kusadzakhalaponso moyo wake wonse. Iyo ikhoza kukhala pa mkazi *uyu* usiku wotsatira. Mwinamwake pa mwamuna *uyu* nthawi yotsatira. Mwinamwake pa *uyo* kumbuyo uko, nthawi ina. Zimenezo sizimamupanga iye kukhala mneneri, sizimamupanga aliyense kukhala mneneri. Iyo ndi *mphatso* ya uneneri mwa inu.

⁷¹ Ndipo munthu ameneyo kapena uneneri umenewo usanaperekedwe kwa mpingo, iwo umayenera kuweruzidwa pakati pa oweruza auzimu awiri kapena atatu. Nkulondola uko? Mogwirizana, tsopano, Paulo anati, “Inu nonse mukhoza kumanenera, mmodzi mmodzi.” Ngati chinachake chaululidwa kwa *uyu*, mulole *uyo* akhale bata. Chabwino, izo zikhoza kupanga gulu lonselo kukhala aneneri ndiye, molingana ndi kaphunzitsidwe ka lero. Ayi, mpingo wa Pentekoste, ife tazisokoneza zinthu zonsezo. Ndipo ndicho chifukwa chimene Mulungu sangabweremo, mpaka ife titachikonza chinthucho ndi kukhala pa Baibulo. Uko nkulondola. Inu mukuyenera kutenga njira yolondola. Inu mungamange bwanji nyumba popanda

kuyang'ana pulani? Mukuona? Inu mukuyenera kuyamba moyenera.

⁷² Tsopano, mmenemo, mneneri, inu simunayambe mwamuwonapo aliyense ataima pamaso pa Yesaya, Mose. Mmodzi anaimapo, Korah, tsiku lina, ndipo anayesera kuti atsutsane ndi iye, ndipo Mulungu anati, “Dzipatule wekha, Ine nditsegula nthaka ndipo. . .” Mneneri amachita kubadwa. “Mphatso ndi maitanidwe. . .-panda kulapa.” Kumeneko ndiko kudzozeratu kwa Mulungu, kuyambira ali khanda nkumakula. Chirichonse chinali cholondola mwangwirowi, ndendende chimene iye ananena kuti chinali choonadi ndi chotsimikiziridwa ndi kutulutsidwa. Iwo ndi Mawu a Mulungu, amabwera kwa mneneri. Koma mphatso ya uneneri imakhala mu mpingo.

⁷³ Tsopano inu mukuti, “Chabwino, aneneri ndi a Chipangano Chakale.” Oh, ayi! Chipangano Chatsopano chinali ndi aneneri.

⁷⁴ Agabasi anali—anali mneneri wa Chipangano Chatsopano. Taonani Mzimu wa uneneri ukugwa pansu pamenepo ndi kumuuzza Paulo za izo. Kenako apa panabwera Agabasi akuchokera ku Yerusalemu, ndipo anamupeza Paulo, ndipo anamanga lamba wake pa iye, ndipo anatembenuka ndipo anati, “PAKUTI ATERO AMBUYE, munthu amene anavala ichi akamangidwa ndi unyolo pamene iye akafika ku Yerusalemu.” Agabasi, amene anaimirira ndi kunena, ananeneratu chimene chikanadzachitika, iye anali mneneri, osati munthu wa mphatso ya uneneri.

⁷⁵ Ndipo mphatso ya machiritso ndi mphatso zonsezo, mzanga wa Chipentekoste, iwe wazisokoneza izo. Mphatso zimakhala mu mpingo, ndi za munthu aliyense mu mpingomo, aliyense amene anabatizidwa kulowa mu Thupi. “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwira mkati.” Ndipo Baibulo linati. . .

“Chabwino, ine ndiri ndi mphatso ya machiritso.”

⁷⁶ Chabwino, Baibulo linati, “Vomerezani zolakwa zanu kwa wina ndi mzake, ndipo mupemphererane wina ndi mzake.” Munthu aliyense apempherere wina ndi mzake. Ife si gulu logawanikana; ife ndi gulu lathunthu, gulu losonkhanitsidwa. Mukuona?

Tsopano, ndipo pamenepo ndi mmene ziwanda nthawizina zimagwirira ntchito.

⁷⁷ Tsopano penyani chimene Paulo ananena, “Ngati wina ayankhula ndi malirime ndipo wina nkutanthauzira, ndipo chirichonse chimene iye wanena, icho chiweruzidwe poyamba mpingo usanachilandire icho.”

⁷⁸ Tsopano, izo sizidzakhala kubwereza kwa Lemba, kapena chinachake chimzake ngati chimenecho. Mulungu samadzibwereza Yekha. Koma ilo likhala chenjezo kwa mpingo. Ndiye ngati oweruza abwino anena, “Tiyeni tilandire icho.”

Chabwino, icho chinali cha Ambuye. Wachiwiri ndikuti, “Tiyeni tilandire icho.” “Pakamwa pa mboni ziwiri kapena zitatu, mulole mawu aliwonse akhazikitsidwe.” Kenako mpingo ulandire icho ndipo upite ndikukakonzekera icho. Ngati icho sichikwaniritsidwa, chimene uja unanena, ndiye kuti inu muli ndi mzimu woyipa pakati panu. Uko nkulondola. Ndipo ngati icho chingakwaniritsidwe, ndiye muthokozeni Mulungu, Mzimu wa Mulungu uli pakati panu. Mukuona? Tsopano, pamene ndi pamene inu mukuyenera kupenyetsa ndi kukhala osamalitsa. Chotero, musamayesere kukakamiza. Ine sindikanadzipanga ndekha kukhala ndi maso a bulauni pamene ine ndiri ndi a buluu, mwaona, ine ndikuyenera kukhala wokhutitsidwa ndi maso a buluu. Tsopano, pamene ndi pamene ziwanda zimagwira ntchito mu dera lauzimu.

⁷⁹ Tsopano ife tiri ndi chinachake chakuya chimene chikubwera apa, ndipo ine ndikuyembekezera kuti icho si chakuya kwambiri. Tsopano mu Samuele Woyamba 28, ine ndikufuna kuti ndiwerenge Lemba lina apa pa nthawi ino. Ine ndikufuna kuti inu mumvetsere mwacheru. Ndipo ine ndikufuna ndibweretse “ziwanda,” ndikuwonetseni inu mmene izo zimagwirira ntchito mu mpingo, ndi mmene Satana wakhalira ndi chonyengezera cha chenicheni chirichonse chimene chiripo. Tsopano inu mukhoza kuwona, mogwirizana ndi Baibulo, kuti ziwanda zimabwera pakati pa Akhristu ndipo izo zimatsanzira.

⁸⁰ Ndipo nthawi zambiri ife tawanena anthu kuti ndi Akhristu pamene iwo anena kuti, “Ine ndimakhulupirira mwa Yesu Khristu.” Bwanji, ziwanda zimakhulupirira chinthu chomwecho, ndipo zimanjenjemera. Icho si chizindikiro choti mwapulumsidwa. Umodzi wa mausiku awa ine ndikufuna ndidzafike pa kusankhidwa, ndipo kenako inu mudzawona chimene chipulumutso chimatanthauza. Mukuona? Si kanthu kamene inu muyenera kuchita pa izo, pamalo oyambirira, kapena malo omalizira, kapena kalikonse kamene inu mungathe kuchita za izo. Mulungu amamupulumutsa munthu, mopanda mangawa. Mnyamata, zimenezo zalowa mwakuya, sichoncho izo? Tsopano, zikhoza kuchotsa izo mu chochitika chanu, pamene ife tiri pa zimenezo. Chabwino.

⁸¹ Abrahamu anali chiyambi cha chikhulupiriro chathu. Nkulondola uko? Oh, Abrahamu anali ndi lonjezo. Ndipo Mulungu anamuitana Abrahamu chifukwa chakuti anali mwamuna wopambana, ine ndikuganiza? Ayi, bwana. Iye anabwera kuchokera ku Babeloni, mu—mu dziko la Akadiya, mu mzinda wa Ur, ndipo Mulungu anamuitana iye ndipo anapanga pangano Lake ndi iye, mopanda mangawa. “Ine ndidzakupulumutsa iwe. Ndipo osati iwe wekha, Abrahamu, koma Mbewu yako,” mopanda mangawa.

⁸² Mulungu anapanga pangano ndi munthu, ndipo munthu amaswa pangano lake nthawi iliyonse; munthu sanayambe wasungapo nkomwe pangano lake ndi Mulungu (Lamulo silimasungidwa nkomwe; iwo samatha kusunga lamulo; Khristu anabwera ndipo anadzaswa lamulo, Iyemwini.) chifukwa chisomo chinali chitapereka kale mpulumutsi, Mose, anapereka njira yothawirapo, ndipo kenako, kuthawako kani, ndipo kenako anthuwo, zitatha zimenezo, iwo ankafunabe chinachake choti azichita. Munthu nthawizonse amayesera kuchita chinachake kuti adzipulumutse yekha, pamene inu simungachite zimenezo. Icho ndi chikhalidwe chake. Mwamsanga atangozindikira kuti iye anali maliseche, mmunda wa Edeni, iye anapanga matewera ena a tsamba la mkuyu. Nkulondola uko? Koma iye anapeza kuti iwo samagwira ntchito. Palibe chirichonse chimene munthu angakhoze kuchita chimene chingakupulumutse iwemwini. Mulungu amakupulumutsa iwe, mopanda mangawa, kudutsa m'mibadwo yonse. Ndiyeno pamene iwe wapulumutsidwa, iwe wapulumutsidwa.

⁸³ Tamuwonani Abrahamu. Kumeneko munthu ameneyo anali, anapitako, ndipo Mulungu anamupatsa iye dziko la Palestina ndipo anamuza iye kuti asadzachoke kumeneko. Myuda aliyense amene achoka ku Palestina amakhala wobwerera mmbuyo. Mulungu anamuza iye kuti azikhala kumeneko. Ngati Mulungu akuza iwe kuti uchite chinachake, ndipo iwe nkusachita izo, ndiye kuti iwe wabwerera mmbuyo. Nkulondola uko? Chabwino, chilala chinabwera, kuti chidzayese chikhulupiriro cha Abrahamu. Ndipo mmalo moti Abrahamu akhale kumeneko, ayi, iye sanakhale kumeneko, iye anathawa, ndipo anamutenga Sarah ndipo anapita pafupifupi mailosi firii handiredi (ndikanakonda ndikanakhala ndi nthawi kuti ndifike pa zimenezo) kutsika kupita ku dziko lina.

⁸⁴ Ndipo pamene iye anakafika kumeneko, ndipo atatero anakapeza mfumu yaikulu iyi kumeneko, Abimeleki. Iye anali mwamuna wachichepere ndipo iye ankafuna mkazi, chotero iye anamupeza mkazi wa Abrahamu, Sarah, ndipo anagwa mu chikondi ndi iye. Ndipo Abrahamu anati, “Tsopano, iwe umuuzi iye kuti iwe ndi mchemwali wanga ndipo ndine mchimwene wako.”

⁸⁵ Chotero zimenezo zinamukondweretsa Abimeleki, chotero iye anati, “Chabwino, ife tingomutengera iye ku nyumba yachifumu.” Ndipo ine ndikuganiza akaziwo anamukonzekeretsa iye, ndipo iye anali woti amukwatira iye tsiku lotsatira.

⁸⁶ Ndipo Abimeleki anali mwamuna wabwino, mwamuna wolungama. Ndipo usiku umenewo, pamene iye anali kugona, Ambuye anawonekera kwa iye ndipo anati, “Iwe uli ngati munthu wakufa.” Iye anati, “Mwamunayo. . . Mkazi amene iwe

wamutenga uko kuti umukwatire, ndi mkazi wa mwamuna wina.” Tsopano penyani. “Mkazi wa mwamuna wina.”

⁸⁷ Bwanji, iye anati, “Ambuye, Inu mukudziwa kukhulupirika kwa mtima wanga,” munthu wolungama, munthu woyera. “Inu mukudziwa kukhulupirika kwa mtima wanga. Mwamuna ameneyo anandiuza ine kuti ameneyo ndi ‘mchemwali’ wake. Ndipo kodi iye sanandiuze ine, yekha, kuti uyo ndi ‘mchimwene wanga?’”

⁸⁸ Iye anati, Mulungu anati, “Ine ndikudziwa kukhulupirika kwa mtima wako, ndipo ndi chifukwa chake Ine ndakupulumutsa iwe kuti usandichimwire Ine. Koma ameneyo ndi mneneri Wanga!” Aleluya!

⁸⁹ Kodi iye anali chiyani? Wobwerera mmbuyo, ndiponso wothyathyalika wamng’ono, wabodza. Nkulondola uko? Oh, ayi, palibepo mabodza aang’ono oyera. Iwo amakhala mwina mabodza akuda kapena iwo si mabodza nkomwe. Mwamunayo wakhala kunja uko akunena bodza lankunkhuniza, akunena kuti ameneyo ndi “mchemwali” wake pamene anali mkazi wake, akungozembazemba, ndipo wabwerera mmbuyo.

⁹⁰ Ndipo apa panali mwamuna wolungama atayima pamaso pa Mulungu, ndipo anati, “Ambuye, Inu mukuwudziwa mtima wanga.”

⁹¹ “Koma Ine sindimva pemphero lako, Abimeleki, koma umutenge iye. . . ukamubwezere iye ndipo ukamulole iye kuti akupempherere iwe. Iye ndi mneneri Wanga; Ine ndimumvera iye.” Eya, wobwerera mmbuyo, wabodza, koma, “Ameneyo ndi mneneri Wanga.” Icho ndi Choonadi? Ndiro Baibulo.

⁹² Tsopano, musapite kutali kwambiri apa ku mbali ya Achikalvini, “Kamodzi mu chisomo, nthawizonse mu chisomo,” chifukwa inu mudzalowa mu chitongo. Mukuona? Tsopano, mphindi chabe, ife tipeza nthawi iyi sabata ino kuti tibweretse izo ndi kukuwonetsani inu mmene izo zikukhalira. Koma musamaganize kuti basi chifukwa choti iwe wachita chinachake cholakwika kuti basi iwe wapitiratu mpaka kalekale. Ndiwe mwana wa Mulungu, ndiwe wobadwa mwa Mzimu wa Mulungu, ndinu ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, ndipo zipatso zimadzichitira umboni zokha. Ndi zimenezotu.

⁹³ Tsopano, ndi ife apa, takhala mu dziko. Tsopano, ine ndikufuna kuti ndiwerenge apa, pa ndime ya 6.

Ndipo pamene Sauli anafunsira kwa AMBUYE, AMBUYE sanamuyankhe iye, ngakhale ndi maloto, kapena ndi Urimu, kapena ndi mneneri.

Ndipo kenako Sauli anati kwa antchito ake, Ndifunsireni ine mkazi wa mzimu wobwebweta, kuti ine ndipite kwa iye, ndipo ndikamufunse iye.

Ine ndikhoza kuyika chinachake pa ndodo apa, kwa basi . . .
 “Ndifunireni ine mkazi wa mzimu wobwebweta.”

. . . Ndipo wantchito wake anati kwa iye, Taonani, pali mkazi amene ali ndi mzimu wobwebweta mu En-dor.

Ndipo Sauli anazibisa yekha, ndipo anavala chovala, zovala zina, ndipo iye anapita, awiri . . . ndi amuna awiri ndi iye, ndipo iwo anabwera kwa mkaziyo usiku: ndipo iwo anati, ine ndikukupempha iwe, . . . -tsere kwa ine ndi mzimu wako wobwebweta, ndipo undibweretsere ine . . . ukwere, amene ine nditamutchule kwa iwe.

Ndipo mkaziyo anati kwa iye, Taonani, inu mukudziwa chimene Sauli wachita, mukudziwa, wadula onse amene ali ndi mizimu yobwebweta, ndi . . . afiti, kuwatulutsa mdziko: chotero . . . inu mukundiikira khwekhwe pa moyo wanga, ndi kundipangitsa ine kuti ndife?

Ndipo Sauli anayankha, analumbira kwa iye pa AMBUYE, kuti, Pali Ambuye, palibe chilango chimene chiti chidzachitike kwa iwe . . .

Kenako mkaziyo anati, Ine ndikubweretseni ndani . . . inu? Ndipo iye anati, Ndibweretsere Samuele.

Ndipo pamene mkaziyo anamuona Samuele, iye analira ndi liwu lofuula: ndipo mkaziyo anayankhula kwa Sauli, kuti, Iwe wandinyengeranji ine? pakuti iwe ndi Sauli.

Ndipo mfumu inati kwa iye, Usawope: pakuti iwe waona chiyani? Ndipo mkaziyo anati ine . . . kwa Sauli, ine ndinawona milungu ikukwera kuchokera pa dziko lapansi.

Ndipo iye anati kwa mkaziyo, Iye anali wa maonekedwe otani? Ndipo mkaziyo anati, Mwamuna wokalamba akubwera; ndipo iye waphimbidwa ndi chovala. Ndipo Sam- . . . (Iwo ndi mwinjiro wa mneneri uja, ndithudi. Mukuona?) . . . anazindikira kuti anali Samuele, ndipo iye anaima ndi . . . ndipo anaweramitsa nkhope yake pansu, ndipo anagwada yekha.

Ndipo Samuele anati kwa Sauli, Nchifukwa chiyani wandisokoneza ine, ndi kundibweretsa ine kuno? Ndipo Sauli anayankha, ndipo anati, Ine ndasautsika kwambiri; chifukwa choti Afilisiti akupanga nkondo ndi ine, ndipo Mulungu wandichokera ine, ndipo sakundiyankha ine, osati ndi mneneri, kapena ndi loto: chotero ine . . . ndinaitanira kwa inu, kuti inu mundidziwitse ine chimene ine ndikuyenera kuchita.

Ndipo *kenako Samuele anati, Chifukwa... iwe ukundifunsa... ine, poona kuti AMBUYE akuchokera iwe, ndipo—ndipo akhala mdani wako?*

Ndipo AMBUYE achita kwa iye, monga iye anayankhulira kwa ine: pakuti AMBUYE ang'amba ufumu wake kuchoka mmanja mwako, ndipo waupereka iwo kwa ngakhale... Davide:

⁹⁴ Tsopano, ambiri a inu, mukudziwa izi. Tsopano ife tikufuna kulowa mkati, ndipo Mulungu atithandize ife tsopano, kwa mphindi zochepa, kuti tilowe mu izi. Tsopano penyani. Kunali munthu, Sauli, amene nthawiina ankatengedwa ngati mneneri, pakuti iye ananenera ndi aneneri. Nkulondola uko, aphunzitsi? Tsopano, apa mwamunayo anabwerera mmbuyo. Nkulondola uko? Koma kumbukirani kumene Samuele ananena kuti iye akanakakhala, ndi iye, tsiku lotsatira. Anapita mwamsanga, mwaona. Chabwino, ngati inu simumulabadira Mulungu, Mulungu adzakuchotsani inu pa dziko lapansi.

⁹⁵ Taonani mu kalata ya Akorinto kumeneko, mmene Paulo anawaikira anthu amenewo mu dongosolo. Iye anati, “Poyamba, ine ndikumuthokoza Mulungu chifukwa cha inu, kuti palibepo zinthu zoterozo pakati panu, ndi zina zotero, ndi mmene kuti—kuti inu simunasowe mphatso yauzimu.” Kuwauza iwo chimene iwo anali, mwapamalo, mwa Khristu. Kenako iye anayamba kuwakhoma iwo nyundo, kuwauza iwo za alaliki awo aakazi, ndi mmene iwo amachitira, ndi mmene iwo ankadyera pa gome la Ambuye.

Ndipo ngakhale mwamuna wina kumagona ndi amayi ake owapeza, ndipo anati kwa mwamuna uyu mwa Khristu, “Mperukeni iye kwa mdierekezi, kuti thupi lake liwonongeke, kuti solo ikapulumsidwe.” Mwaona, ndi zimenezotu, kumupereka iye. Baibulo linati, “Pa chifukwa cha ichi ambiri adwala ndipo afooka pakati panu, ndipo ambiri agona,” apita mwachangu chifukwa cha tchimo. Mulungu anakuchotsani inu panjira; chizindikiro chabwino chakuti inu munali Mkristu, ngati mukanatengedwa.

⁹⁶ Chotero, tsopano zindikirani apa, Sauli ankatengedwa kukhala mmodzi wa aneneri, kapena pakati pa aneneri, chifukwa iye analosera. Ndipo tsopano iye anali atabwerera mmbuyo, chifukwa iye sanamumvere Mulungu, ndipo ufumu wake unang'ambidwa kuchoka mmanja ake ndipo unaikidwa mdzanja la Davide, amene Mulungu anamuzodza ndi Samuele, ndi nsupa ya mafuta.

⁹⁷ Zindikirani, ndiye, panali njira zitatatu zimene iwo anali nazo zopezera zinthu kwa Mulungu; yoyamba inali—inali mneneri, yachiwiri inali maloto, ndipo chachitatu chinali Urimu Tumimu. Ndipo izo sizinkayankha. Tsopano, inu mukudziwa chimene mneneri ali, inu mukudziwa chimene maloto auzimu ali, ndipo

inu mukudziwa chimene Urimu Tumimu inali. Inu mukudziwa, tsiku lina ine ndinamufunsa mu—munthu za Urimu, ndipo munthu ameneyo amalephera kuti andiuze ine chimene iyo inali, Urimu Tumimu. Ndithudi, anali Mulungu akuyankha ndi izi. Mukuona?

⁹⁸ Ndipo mdierekezi amapanga chotsanzira cha chirichonse cha izo; mfiti, mneneri wonyenga, ndi wolosera. Mukuona?

Tsopano, Urimu Tumimu inkapachikidwa pa chifuwa cha Aroni, *apa*, ndipo Urimu Tumimu inkaphimba miyala imeneyo. Ndipo iwo ankaipachika iyo mu kachisi. Ndipo pamene iwo sanali otsimikiza, iwo ankapita pamaso pa Mulungu, kukapeza yankho, ndipo kuwala kunkathwanima pa Urimu Tumimu ameneyo, chimene, ngati icho chinali chifuniro cha Mulungu, kapena ayi. Tsopano, Urimu Tumimu ikapanda kuyankha. . . Tsopano, limenelo linali yankho lolunjika lochokera kwa Mulungu.

Tsopano, Urimu Tumimu wa lero; wambwebwe anatenga mpira wa krustalo, kuti zigwirizane ndi Iwo; chinthu chabodza. Mulungu ali mu utatu; mphamvu za Mulungu ziri mu utatu. Ndipo mdierekezi ali mu utatu, ndipo mphamvu zake ziri mu utatu. Ndipo ine ndikhoza kutsimikizira izo ndi Baibulo. Ndipo Urimu Tumimu imeneyo, a . . . inali mpira wokhawo wa krustale umene mdierekezi amagwiritsa ntchito lero. Ndipo mneneri wabodza wabweranso kuno lero, iye amene ife tiri naye pano, anali, kapena, mfiti, kapena wambwebwe kunja uko, anatenga malo a mneneri, mbali ya mdierekezi. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

⁹⁹ Tsopano, ndiye, Urimu wa Tumimu lero ndi Baibulo. Ngati winawake wapereka uneneri kapena maloto, ndipo izo nkusagwirizana kapena kufanana ndi Baibulo la Mulungu, izo ndi zabodza. Musakhulupirire izo.

¹⁰⁰ Mwamuna anabwera kwa ine osati kale, wochokera ku India, kumene ine ndikukonzekera kuti ndipiteko, mlaliki wabwino wamng'ono. Iye anati, "M'bale Branham, ine ndabwera kuno." Anati, "Mkazi anali ndi Mzimu Woyera, ndipo," anati, "iye anali basi mkazi wokomesetsa, wabwino." Iye anati, "Ndipo iye anali atakwatiwa kanai, ndipo amakhala ndi mwamuna wake wachinayi. Ndipo ine ndinati, 'Chabwino, izo zingatheke bwanji, Ambuye?'" Ndipo anati, "Ine ndinapita kwa Iye ndipo ndinati, 'Oh, ulemelero kwa Mulungu!' Anati, 'Aleluya! Ambuye alemekezeke!'" Basi mmodzi wa mtundu umenewo, inu mukudziwa. "Anati, 'Aleluya! Ambuye alemekezeke!'" Anati, "Ambuye anandiuzza ine, 'Pano, Ine ndikupatsa iwe loto.'" Ndipo anati, "Ine ndinalota kuti mkazi wanga, ine ndinamuwona iye akukhala mu chigololo. Ndipo iye anabwerera kwa ine ndipo anati, 'Oh, iwe undikhululukira ine, Victor? Iwe undikhululukira ine? Ine sindinatero. . . 'Bwanji,' ine ndinati, 'ndithudi, ine

ndikukhululukira iwe ndipo ndikutenganso iwe.” Iye anati, “Tsopano, icho ndi chimene ine ndinachita.” Anati, “Mwaona, ine ndakhululuka.”

¹⁰¹ Ine ndinati, “Victor, maloto ako anali okoma mwamphamvu, koma mdierekezi anakupatsa iwe ilo.”

Iye anati, “Bwanji?”

¹⁰² Ine ndinati, “Sakufanana ndi Mawu a Mulungu. Iye akukhala mu chigololo. Mwamtheradi. Iye sangakhale ndi amuna anai. Kulondola. Iye amasiya zimenezo ndi kubwerera kwa woyambirira wake, iye ndiwoyipa kuposa mmene iye analiri pachiyambi. Iye akuyenera kukhala yekha, moyo wake wonse.” Ine ndinati, “Iwe ukudziwa izo sizikufanana ndi Mawu a Mulungu. Chotero iye. . . Loto lako linali labodza.” Ine ndinati, “Ilo silingafanane ndi Ichi.”

¹⁰³ Ndipo mneneri akapereka ulosi, ndipo iwo nkuyankhula, ndipo akafuna kuwona ngati ulosi umenewo unali wolondola, iwo ankawuika iwo pa Urimu Tumimu. Ndipo ngati Liwu la Mulungu liponyera kuwala pa Urimu Tumimu, ndiye icho chimakhala mtheradi, Choonadi. Ndipo ngati munthu apereka kutanthauzira, apereka loto, apereka chinachake cha mu Baibulo, ndipo, kapena china chakenso, ndipo izo nkusagwirizana ndi Baibulo la Mulungu, izo ndi zabodza. Pamenepo pali Urimu Tumimu lero. Mawu a Mulungu amayankhula, ndipo ndiro Liwu la Mulungu lolunjika, monga Urimu Tumimu ankakhalira Baibulo lisanalembedwe. Amen! Aleluya! Ine ndikumverera ngati mwachipembedzo pakali pano. Musanditenge ine ngati wotengeka, ngati inu mukutero. Ine ndikudziwa, ine ndikudziwa pamene ine ndiri. Ine sikuti ndatengeka. Uko nkulondola.

¹⁰⁴ Apa pali Choonadi, Mawu a Mulungu! Ine sindikusamala kuti ndi mtundu wanji wa loto umene inu munali nawo, kapena ndi mtundu wanji wa ulosi umene munapereka, ngati izo si Mawu a Mulungu, izo ndi zolakwika, ngati izo sizikufanana ndi Mawu amenewo. Ndiro limene liri vuto lero. Wina amakhala ndi loto, wina amakhala ndi masomphenya, wina amakhala ndi lirime, wina amakhala ndi vumbulutso; izo zimasokoneza chinthu chonsecho ndi chirichonse, inu muli ndi zipembedzo ndipo mumaphwasula chirichonse. Inu mukuyenera kuzibwezeretsa izo ku maziko omaliza, ndipo amenewo ndi Mawu a Mulungu. Ndizo zoono.

¹⁰⁵ Mipingo imamangidwa pa mmodzi, anati, “Oh, Yesu akubwera pa kavalo woyera. Ine ndikudziwa. Ine ndamuwona Iye mu masomphenya.” Iwo amapanga mpingo wa mtundu umenewo. “Oh, aleluya! Iye akubwera pa mtambo.” Iwo amazipanga izo mu mtundu wotero. Kuziphwasula izo, ndi kuzilekanitsa, ndi kumatchulana wina ndi mzake “chisa cha akhungubwe,” ndi “kokhala nsabwe,” ndi chirichonse monga

choncho. Bwanji, m'bale, izo zimawonetsera, poyambirira pomwe, mtima wanu suli bwino ndi Mulungu pamene inu muchita zimenezo. Uko nkulondola. Ife ndi abale. Ife tikuyenera kumamatirana wina ndi mzake. Ife timasowana wina ndi mzake.

¹⁰⁶ Tsopano taonani. Sauli anali atabwerera mmbuyo, ndipo iye akupita mmwamba. Iye, Mulungu, anali atatembenuza nkhope Yake kuchoka kwa iye. Ndipo iye anapitako ndipo anakafunsira kwa aneneri. Aneneri anapita ndipo anakayesera kuti anenere, ndipo Mulungu anadula, sanapereke masomphenya. Mneneri anatuluka, anati, "Ine sindingathe. Ayi. Iye sanandiuze ine kalikonse ka iwe."

¹⁰⁷ Chabwino, kenako iye anati, "Ambuye, ndipatseni ine loto." Usiku ndi usiku, maloto sanabwere.

¹⁰⁸ Kenako iye anapita mu Urimu Tumimu, ndipo iye anati, "O Mulungu! Ine ndawayesa aneneri, Ine ndayerapo maloto, tsopano Inu mundithandize ine. Kodi Inu muchita zimenezo?" Anadula izo, panalibe Kuwala kunathwanima nkomwe.

¹⁰⁹ Kenako iye anaganiza zopita kwa mfiti, wotsika, wonyozedwa. Ndipo iye anapita kwa iye, ndipo anakwawira mmenemo ndipo anadzizimbaita yekha. Ndipo mfiti iyi inapita ndipo inakaitana mzimu wa Samuele.

¹¹⁰ Tsopano, ine ndikudziwa chimene inu mukuganiza. Ambiri anati, "Ameneyo sanali Samuele." Koma Baibulo linati anali Samuele, ndipo anali Samuele. Ndi zachirendo mmene inu mukumvetsera izo, kuti sichoncho? Koma ameneyo anali Samuele. Baibulo linanena choncho.

¹¹¹ Ndipo mfiti imeneyo imakhoza kumuitana iye, ndipo iye anamuitana Samuele. Ndipo Samuele anali kwina kwakenso, koma ankadziwa zimene zimachitika, ndipo anali atayimabe atavala mwinjiro wake wa mneneri. Chotero, m'bale, pamene inu mufa, inu simunafe, inu mukukhala moyo kwinakwake, kwina kwakenso.

¹¹² Ndiloleni ine ndiime miniti chabe, kuti ndilitengere phunziro la ziwanda ili pansu pang'ono chabe. Iye anali chiwanda, koma iye anali wolumikizana kwambiri ndi dziko la zauzimu. Tsopano, lero, kuli azamizimu ambiri amene amadziwa kwenikweni zochuluka za dziko lauzimu kuposa anthu amene amadzinenera okha kuti ndi Akhristu, komabe iye ndi chiwanda. Mu nthawi za Baibulo zinali chinthu chomwe chomwecho.

¹¹³ Pamene Yesu anali kuno pa dziko lapansi, kunali mapurofesa amenewo ndi masikolala ndi aphunzitsi, ena apamwamba amene analipo, ochokera ku maseminare abwino kuposa amene ife tingakhale nawo lero. Ndipo amuna oyera, odziwika, iwo ankayenera kukhala. Ngati Mlevi apezeka, iye amayenera kukhala wopanda banga, worungama mu njira iliyonse. Ndipo komabe mwamuna ameneyo sankadziwa zochuluka za Mulungu monga kalulu amadziwira za nsapato za chisanu. Pamene

Yesu anabwera, iye analephera kuti amuzindikire Iye, ndipo anamutcha Yesu “mdierekezi.” Iye anati, “Iye ndi Bezezebule, kalonga wa mdierekezi.” Nkulondola uko?

¹¹⁴ Ndipo apa panabwera mtundu wotsikitsitsa wa chiwanda, chimene chinamumangirira munthu kunja uko kumanda, ndi chirichonse, ndipo izo zinaitana. Mdierekezi mwiniwake anati, “Ife tikudziwa Yemwe Iwe uli. Ndiwe Mwana wa Mulungu, Woyera Uyo.” Nkulondola uko? Mfiti zazikazi ndi mfiti zazimuna, ziwanda, zinamuzindikira Iye Mwana wa Mulungu; pamene ophunzira, alaliki afioloje aku seminare anamuzindikira Iye kuti ndi Bezezebule. Ankalondola mndani, mdierekezi kapena mlaliki? Mdierekezi amalondola. Ndipo, m’bale, izo sizinasinthe kwambiri lero. Iwo sakuzindikira mphamvu ya Mulungu.

¹¹⁵ Ziribe kanthu kuti muli ndi kuphunzitsa kochuluka bwanji, mungaziyike zimenezo mwa inu. Mulungu samakhala mu mawu aakulu. Mulungu amakhala mu mtima wona. Inu mukhoza kuyima apa, kuyankhula mawu aakulu, ngati sindikudziwa chiyani, izo sizimakubweretsani inu pafupi ndi Mulungu. Inu mukhoza kuimirira ndi kuphunzira momwe mungabwerezere ulaliki wanu ndi kunena zinthu izi, zimenezo sizimakubweretsani inu pafupi ndi Mulungu. Inu mukhoza kuphunzira dikishonare mpaka kugona ndi imodzi, ndipo iyo siingakubweretsenibe inu pafupi ndi Mulungu. Mtima wodzichepetsa, wodzipereka, mu kuphweka, ndi umene umakubweretsani inu kwa Mulungu. Ndipo izo nzoona. Amen! Mtima wodzichepetsa, Mulungu amawukonda. Tsopano, ziribe kanthu ngati iwe sukudziwa ma ABC ako, izo sizimapanga kusiyana kulikonse. Basi mtima wodzichepetsa! Mulungu amakhala mu mtima wodzichepetsa; osati mu maphunziro, si mmasukulu, osati mu zaumulungu, maseminare, osati mu malo onse awa osiyanasiyana; osati mu mawu aakulu, kapena osati mmalo apamwamba. Mulungu amakhala mu mtima wa munthu. Ndipo modzichepetsa mmene mungadziswere pansi nokha, mophweka kwambiri, mukhoza kukhala wamkulu pamaso pa Mulungu.

¹¹⁶ Mundilole ine ndikupatseni inu chinachake. Ine ndikuwona minda yanu yadzaza tirigu kunja kuno. Mutu wathunthu wa tirigu nthawi zonse umawerama. Katsamba kakale kakang’ono kamamatirira pamwamba pamenepo, ndi kumafufuma mozungulira ngati kuti kakudziwa chirichonse, iko kalibe icho mmutu. Ndi momwe ziliri ndi anyamata ambiriwa amene amaganiza kuti ali ndi zochuluka mmutu mwawo, ndipo alibe chirichonse mu mtima mwawo, ngakhalebe. Mutu woyera umawerama ku Mphamvu, umazindikira Yesu Khristu ngati Mwana wa Mulungu, ndi kukhulupirira ntchito Zake.

¹¹⁷ “Ndipo Iye ali yemweyo, dzulo.” Oh, iwo amamuzindikira Iye, ndithudi, mu mawonedwe a mbiriyakale. Koma si chinthu cha mbiriyakale. Anthu amaimirira ndikuti, “Oh, ine

ndimakhulupirira Pentekoste, pamene iwo anali ndi kutsanulira kwakukulu ndi zinthu monga zimenezo,” ndi kujambula moto. Munthu wozidwa sangathetsedwe ndi moto wojambula. Moto wojambula sumatentha. Icho ndi chimene izo zinali. Ndi chiyani lero, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero ndi kwanthawizonse? Umenewo ndi moto wojambula. Munthu wina atazidwa mpaka kufuna kufa, anati, “Taonani moto wawukulu uwo umene iwo anali nawo.” Bwanji, umenewo sumakutenthsa iwe.

¹¹⁸ Chimene iwo anachita pa Pentekoste, chimene iwo anali nacho mu Chipangano choyambirira, ife tiri nacho lero! Ndipo mwamsanga pamene Mulungu achiwongola chinthucho, ndipo Mpingo nkukhala pamodzi, Mkwatulo udzabwera. Koma timalephera ngakhale kuti tikhale ndi chikhulupiriro cha machiritso Auzimu, osatinso Mkwatulo, chifukwa ife tonse tapiringizidwa, wina njira *iyi* ndi wina njira *iyi*. “Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti* anati Ichi chinali *ichi*. Chabwino, mlaliki wanga anati Iye anali *Ichi*.”

¹¹⁹ Kanthawi kapitako, mkazi anati, “Iye ndi wonyenga chabe.” Anati, “Wansembe wanga anandiuza ine chomwecho.” Ine ndikanakonda wansembe wakeyo akanabwera kuno kamodzi, ife tikanawona yemwe ali wonyenga. Eya. Tidzawona yemwe ali wonyenga. Abwera adzayese izo.

¹²⁰ Kuno osati kale kwambiri, ku Harlingen, Texas, ife tinali ndi msonkhano kumeneko. Ndipo iwo anali ndi zikwangwani zazikulu, paliponse kunjira pa magalimoto usiku uja pamene ine ndinapita kumeneko, ananena kuti a FBI anali kumeneko kuti andiyaluse ine ngati wachinyengo. Chotero mtsikana wamng’ono anali atachiritsidwa ku Texas uko kwina kwake. Iye anali kumtunda uko, ndipo, ine—ine ndikuganiza, pafupifupi mailosi sauzande, kumtunda uko kufupi ndi Panhandle. Ndipo izi zinali kumusi ku Harlingen, kumusi kumalire. M’bale Baxter anabwera, anati, “M’bale Branham,” anati, “inu simunayambe mwawonapo chisokonezo choterocho kumusi uko, pafupifupi anthu foro kapena faivi sauzande.” Ndipo anati, “Ndiyeno, kuzungulira paliponse, a FBI akakugwirani inu pa nsanja usikuuno, ndipo akakuyalutsani inu.”

Ine ndinati, “Chabwino, ndine wokondwa ndithudi ndi zimenezo.”

¹²¹ Anati, “Inu mukumudziwa mtsikana wamng’ono uja yemwe anachiritsidwa usiku wina?”

¹²² Ine ndinali ndikubwera kunyumba kuchokera . . . ndikupita mchipinda changa. Ndinamva chinachake chikulira, ndipo ndinayang’ana pozungulira. Ine ndimaganiza kuti mwinamwake wina wachitidwa chiwembu. Iye anali mtsikana. Ndipo ine ndinayang’ana mmbuyo. Ine ndinati . . . Ndipo ine ndinabwerera mmbuyo, ndinati, “Chavuta ndi chiyani, Adona?” Ndipo anali

atsikana awiri aang’ono ataima pamenepo, pafupifupi usinkhu wa zaka seventini, eyitini zakubadwa, aliyense, mikono yawo atakumbatirana wina ndi mzake, akulira.

123 Anati, “M’bale Branham!” Ine ndinadziwa pamenepo kuti iwo amandidziwa ine. Anati, “Ife, ine ndamubweretsa iye njira yonse kumusi kuno.” Anati, “Iye akuyenera kuti apite ku malo azamisala.” Ndipo mtsikana wamng’onyo anali mu msonkhano wanga uko ku Lubbock, Texas. Ndipo anati, “Ine ndimadziwa kuti ngati ine ndingamubweretse iye kuno ndipo inu mukanakhala ndi pemphero kwa iye, ine ndikukhulupirira Mulungu akanamuchiritsa iye.”

124 Chabwino, ine ndinaganiza, “Chikhulupiriro bwanji!” Ndipo ine ndinati, “Chabwino, tsopano, mlongo, kodi inu mungakamutenge iye. . .” Ndipo basi pomwepo ine ndinati, “Inu mwabwera kuno mu galimoto yachikasu, sichoncho inu?”

Anati, “Inde!”

Ndipo ine ndinati, “Amayi anu ndi odwalika.”

Iye anati, “Uko nkulondola.”

Ine ndinati, “Ndinu wa mpingo wa Methodisti.”

Iye anati, “Izo ndi ndendende zoonu.”

125 Ndipo ine ndinati, “Mukubwera pa msewu, inu munatsala pang’ono kutembenezika. Iwe ndi mtsikana uyu mumaseka pamene mumabwera pamene panali theka la konkire ndi theka phula, ndipo inu mumatembenuka pokhota.”

Iye anati, “M’bale Branham, zimenezo ndi zoonu!”

Ine ndinati, “Ndipo, PAKUTI ATERO AMBUYE, mtsikanayo wachiritsidwa.”

126 Tsiku lotsatira iye anali akuyatsa moto mtawunimo, akumuza aliyense, akuyendayenda ndi zimenezo. Ndithudi, iwo samamudziwa iye kumeneko, ngati iye anayamba wakhalapo mu chikhalidwe chimenecho kapena ayi. Ndiyeno tsiku limenelo ine. . . M’bale Baxter anati, “M’bale Branham,” anati, “atsikana aja ali kumusi uko akulongeza chikwama chawo.” Ndipo ichi ndi chinthu chimodzi chimene iye samadziwa kuti ine ndimachidziwa. Chuma chathu chinali chitatsika pansi. Ine sindinamulole iye kuti ayankhule za izo. Koma mmodzi wa atsikana amenewo anali ataika madola naini handiredi mmenemo—mu chopereka chimenecho usiku wa pambuyo pake, ndipo anazichulukitsa ndalamazo. Tsopano, iye samadziwa, iye sakudziwa izo mpaka lero, koma ine ndinadziwa zimenezo. Mukuona? Kuti ine. . . Mulungu anandiuza ine kuti zikhala bwino.

127 Ndipo M’bale Baxter anati, “M’bale Branham,” anati, “kulibwino mundirole ine ndikoke pang’ono.” Anati, “Iwo

anakhalapo nawo ena a awa kuno ochiritsa Auzimu kumusi kuno amene amangowakoka anthu awa.”

128 Ine ndinati, “Palibe. Ayi, bwana. Inu simuchita zimenezo. M’bale Baxter, nthawi imene mungapange chikoka cha ndalama monga choncho, ndiyo nthawi imene inu ndi ine tidzangogwirana chanza ngati abale, ine ndizidzapita ndekha.” Mukuona? Ine ndinati, “Musamachite zimenezo.” Ine ndinati, “Mulungu ali ndi ng’ombe pa mapiri sauzande, ndipo chirichonse ndi Chake. Ine ndi wa Iye. Iye adzandisamalira ine.”

Iye anati, “Chabwino.”

129 Ndipo usiku womwewo iye anati, “M’bale Branham, tayang’anani kuno. Winawake... Tayang’anani kuno! Pali envelopu apa, yopanda dzina, ili ndi ma wani handiredi dolla naini mmenemo. Ndendende basi zomwe tikufunikira kuti tikhale nazo.”

Ine ndinati, “M’bale Baxter.”

Iye anati, “Mundikhululukire ine.”

130 Chotero ndiye ine ndinadziwa kuti anali mtsikana uja. Chotero ndiye—ndiye tsiku lotsatiralo, M’bale Baxter anati, “M’bale Branham, iwo ali kumusi uko akulongeza zovala zawo, akulira.”

Ine ndinati, “Chavuta ndi chiyani?”

Anati, “Inu kulibwino mupiteko ndipo mukawawone iwo.”

131 Ine ndinapita mmusi ku chipinda komwe iwo anali. Ine ndinati, “Iwo ali mchipinda chiti?” Ine ndinapita kumeneko ndipo ndinagogoda pakhomo. Ine ndinawamva iwo akulira. Ine ndinagogoda pa chitseko, ndipo mtsikanayo anabwera pa khomo, iye anati, “Oh, M’bale Branham, ine ndikupepesa.” Iye anati, “Ine ndakubweretserani inu mavuto onsewa.”

Ine ndinati, “Mavuto? Chavuta ndi chiyani, mlongo?”

Iye anati, “Oh, a FBI akukufunani inu.”

Ndipo ine ndinati, “Oh, ziri chomwecho?”

132 Anati, “Eya.” Anati, “Ine ndikuganiza ine ndinachitira umboni kwambiri kuzungulira tawuni lero, ndi chirichonse.”

Ine ndinati, “Ayi.”

133 Ndipo iye anati, “M’bale Branham, a FBI ali kumeneko, ali kumeneko, akuti akuyalutsani inu usikuuno.”

134 Ine ndinati, “Chabwino, ngati ine—ngati ine ndikuchita chirichonse cholakwika, ine ndikusowa kuti ndiyalutsidwe.” Mukuona? Ine ndinati, “Ndithudi. Ngati kulalikirira Uthenga kukuyenera kuyalutsidwa, chabwino, tiyeni tichite zimenezo.” Mukuona? Ine ndinati, “Ine—ine—ine ndimakhala moyo mogwirizana ndi Baibulo ili, ndipo zimene Baibulo ili

silimanena. . . Ili ndi chodzitetezera changa, pomwe pano.” Mukuona? Ndipo ine ndinati, ndipo iye. . .

Iye anati, “Chabwino,” anati, “Inu ndikungopepesa kuti ndinachita zomwe ndinachita.”

Ine ndinati, “Iwe sunachite kalikonse, mlongo.”

Iye anati, “Chabwino, inu simukuchita mantha kupita kumeneko?”

Ndipo ine ndinati, “Ayi.”

Iye anati, “Chabwino, a FBI ali kumeneko.”

¹³⁵ Ine ndinati, “Chabwino, iwo anayamba abwerapo mu msonkhano wanga ndipo iwo anapulumsidwa.” Ine ndinati, “Bambo Al Farrar. . .”

¹³⁶ Kaputeni Al Farrar, ambiri a inu mukudziwa za kutembenuka kwake uko mu Tacoma, Washington, anapulumsidwa, kumusi uko ku bwalo la chandamale. Anabwera mu msonkhano, iye anati, “Ine ndamutsatira munthu uyu kwa zaka ziwiri. Ndipo ine ndinamva za ndalama, ndipo ine ndakhala ndikuziyang’ana izo, ndipo ndinapita kulikonse.” Ndipo anati, “Icho ndi Choonadi, inu simukumvetsera kwa wotengeka usikuuno, inu mukumvetsera kwa Choonadi.” Anati, “Mmodzi wa amuna a ku polisi, amene ine ndinati adokotala akamuyang’ane mwana wake ndi kumutumiza iye adutse pamzere wa pemphero,” ndipo anati, “mwanayo anauzidwa ndendende chimene chimamuvuta, ndi chimene chinachitika kwa iye. Ndipo anati, ‘Mu masiku eyiti iye abwerera ku sukulu,’” vuto lopuwala. Ndipo anati, “Pa tsiku la eyiti mwanayo anabwerera ku sukulu.” Anati, “Ine ndamutsatira iye kwa zaka ziwiri,” pamaso pa anthu teni sauzande. Ndi zimenezo zonse. . . Pali chithunzi cha izo, msonkhano waku Seattle, mu—mu bukhu lanu. Iye anati, “Ine ndikufuna inu nonse mudziwe kuti inu simukumvetsera ku phokoso linalake la chipembedzo. Inu mukumvetsera kwa Choonadi.” Kaputeni Al Farrar. Ndipo tsiku lotsatira ine ndinamutsogolera iye kwa Mulungu, ndipo iye analandira ubatizo wa Mzimu Woyera, mu bwalo la chandamale, kumusi ku malo aakulu kunjani uko.

Ine ndinati, “Mwinamwake munthu uyu achita chimodzimodzi.”

Chotero iye anati, “Kodi inu mukuchita mantha kupita kumeneko?”

¹³⁷ Ine ndinati, “Mantha? Bwanji, ndithudi ayi. Ndithudi ayi. Ine ndichite mantha ndi chiyani pamene Mulungu anandituma ine kuti ndidzachite zimenezo? Ndi Iyeyo amene amamenya nkhoodoyo, osati ine.” Chotero ine ndinati, “Tsopano, ine ndikufuna ine nonse mukhale kutali.” Ndipo chotero. . .

¹³⁸ Iye tinapita ku msonkhano usiku umenewo, malowo anali atadzaza. Ndipo woyang’anira pamalo kumeneko anatulukira,

anati, “M’busa Branham, ine ndapangitsa ganyu ana teni achi Mexico.” Anati, “Taonani apa, M’busa Branham ayalutsidwa usikuuno ndi FBI, wachipembedzo wotengeka,” kapena chinachake monga chimenecho. Ndipo anati, “Izo ziri pa iliyonse ya magalimoto amenewo. Kokani...” Anati, “Ine ndipangitsa ganyu ana teni achi Mexico, apita kukazichotsa zonsezo ndi kudzaziika izo apa.” Anati, “Oh, ine ndikumverera ngati ndikanamupeza mwamuna ameneyo!”

¹³⁹ Ine ndinati, “Musadandaule, bwana. Mulungu amugwira iye.” Mukuona? Ine ndinati, “Mungomusiya iye yekha.”

¹⁴⁰ Chotero iye anadzabwerako. Ndipo usiku umenewo pamene ife tinadzalowa, ine sindidzaiwala konse zimenezo, ndinadzalowa mu chipinda. Ine...M’bale Baxter anaimba *Kungo Khulupirira*. Iye anati, “Tsopano, M’bale Branham akuti usikuuno kuti tichoke mchipindachi.” Anati, “Ine ndikubwerera kumbuyo ndipo ndikakhala pansi.” Iye anati, “Iwo akonzekera kuti amuyalutse iye usikuuno pano pa nsanja.” Iye anati, “Ine ndamuwonapo iye mu nkondo zolimba zambiri, ndipo ndamuwonapo Mulungu akutenga malo ake.” Anati, “Ine—ine ndingobwerera mmbuyo ndikakhale pansi.”

¹⁴¹ Ine ndinayenda kupita chokwera. Ine ndinati, “Ine ndinali ndikuwerenga kankhani kakang’ono apa ya kumene ine ndinali woti ndikayalutsidweko usikuuno pa nsanja kuno.” Ine ndinati, “Ine ndikufuna nthumwi za FBI tsopano kuti zibwere kutsogolo ndi kudzandiyalutsa ine pano pa nsanja.” Ine ndinati, “Ine ndikuima pano potetezera Uthenga; ine ndikufuna kuti inu mubwere ndipo mudzandiyalutse ine.” Ine ndinadikirira. Ine ndinati, “Mwinamwake iwo sanafike pano.” Ine ndimadziwa pamene ine ndinali. Iye anali atandiwonetsera kale mu chipinda changa uko, chimene chikanati chidzachitike, ine ndisanachoke, inu mwaona. Ndipo ine ndinati, ine ndinati, “Mwinamwake ine ndingodikirira pang’ono. Kodi tingaimbe nyimbo?” Ndipo winawake anabwera ndipo anaimba nyimbo yoyimba yekha.

¹⁴² Ine ndinati, “Bambo woimirira FBI, kodi inu muli mkati muno kapena panja? Ine ndikudikirira kuti ndiyalutsidwe. Kodi inu mungabwere kutsogolo?” Palibe anabwera. Ine ndinkangodabwa pamene izo zinali. Ambuye anandiiza ine chimene icho chinali. Iwo anali alaliki awiri obwerera mmbuyo, ndipo ine—ine ndinali ndikupenyetsa. Ine ndinawona mthunzi wakuda pakona. Ine ndinadziwa pamene izo zinali. Ine ndinayang’ana pamenepo, ndipo iwo unasanthira mmwamba ndipo unapita mchipinda cha zaluso monga chonchi. Mwamuna wovala suti ya buluu, wina wavala yotuwa.

¹⁴³ Ine ndinati, “Abwenzi, palibepo a FBI. A FBI ali ndi chochita chanji ndi kulalikira Baibulo?” Ine ndinati, “Ndithudi ayi. Iwo sanali a FBI awiri oti andiyalutse ine. Koma, apa pali kuyalutsa, akhala apo pamwamba kumene apo, alaliki

awiriwo pomwe apo.” Ndipo iwo anawerama pansi. Ine ndinati, “Musawerame pansi monga choncho.” Ndipo awiri achi Texans aakulu amenewo anali akupita kumeneko kuti akawagwire iwo. Ine ndinati, “Ayi, abale, iyi si nkhani ya thupi ndi magazi, ingokhalani bata. Mulungu asamalira izo.”

¹⁴⁴ Ine ndinati, “Tsopano, abale, taonani, pamene inu muli pamenepe, tayang’anani mbali iyi.” Ine ndinati, “Ngati... Inu mumati ine ndi Simoni wamatsenga, pansi pa ufiti, ine ndimawalodza anthu.” Ine ndinati, “Ngati ine ndiri Simoni wamatsenga, ndiye kuti inu ndi munthu wa Mulungu. Tsopano inu mubwere kuno pa nsanja iyi. Ndipo ngati ine ndine Simoni wamatsenga, mulole Mulungu andikanthe ine ndi imfa. Ndipo ngati ine ndiri mneneri wa Mulungu, inu mubwere kuno ndipo Mulungu akukantheni inu ndi imfa. Tsopano ife tiwona amene akulondola ndi amene akulakwitsa. Tsopano mubwere mutsikire kuno. Ife tiimba nyimbo.” Kuchokera mchipindacho anatuluka, ndipo ife sitinawawonenso kuyambira pamenepe. Mukuona? Ine ndinati, “Bwerani. Ngati ndine Simoni wamatsenga, musiyeni Mulungu andikanthe ine ndife. Ndipo ngati ndine mneneri wa Mulungu, ndiye Mulungu akukanthani inu ndi imfa pamene inu mutabwere pa nsanja iyi. Ngati ine ndikulondola pamaso pa Mulungu, Mulungu akusiyani inu kuti mufe pa nsanja pano.” Iwo anali akudziwa bwino. Uko nkulondola. Iwo anali akudziwa bwino. Iwo anali atamva kuchokera ku malo ena. Uko nkulondola. Chotero musamaganize koma kuti Mulungu akadali Mulungu. Iye amayankha.

¹⁴⁵ Tsopano, mfiti yaku En-dori iyi, iye anawuitanitsa mzimu wa Samuele. Ndipo Sauli anayankhula ndi Samuele. Tsopano, inu mukhoza kudabwa mmene izo zingachitikire. Izo zizingachitike lero. Ayi, bwana. Chifukwa, magazi a ng’ombe ndi mbuzi ankadikirira nthawi ya kukwaniritsidwa. Munthu akafa mmasiku amenewo... Alaliki, mundichitire umboni ngati inu mukuganiza kuti Izo ndi zoono. Munthu akafa, iye ankafa pansi pa chitetezero cha nyama, ndipo solo yake inkapita mu Paradiso. Ndipo kumeneko iye ankakhala mpaka limenelo, ku—Tsiku la Chiwombolo. Ndipo solo yake inali mmenemo.

¹⁴⁶ Ndiloloni ine ndikujambulireni inu chithunzi chaching’ono apa. Ndi angati anawerenga nkhani yanga, kapena nkhani imene iwo analemba yokhudza ine mu *Reader’s Digest* kuno, pafupifupi ya mu Okutobala, nkhani ya mu Novembara? Chabwino. Kodi inu munazindikira mmene izo zinkakhalira? Kodi inu munazindikira, pafupifupi masabata awiri kapena atatu izo zisanachitike, wamatsenga wotchuka uyu apa amene wayesedwa kuyambira kalekale, iye, Abiti Piper. Kodi aliyense anayamba wawerengapo izo, nkhani ya Abiti Piper mu *Reader’s Digest*? Izo sizachirendo mmene mizimu iwiri imeneyo... .

¹⁴⁷ Kodi ine ndiri ndi nthawi yochuluka bwanji? Osati koma pang’ono chabe. Ine ndadutsitsa twente, basi ine ndikuyenera

ndifulumire. Ine ndikudziwa inu muli...Tayang'anani, mundikhululukire kwa miniti.

¹⁴⁸ Inu mukudziwa, pali—pali chabodza. Pali choona ndi chabodza cha chirichonse. Ngati ine nditakupatsani inu dolla, ndipo nkuti, “Kodi iyi ndi dolla yabwino?” Ndipo inu mukhoza kuiyang’ana iyo, iyo ingayenere kuti iziwoneka ngati dolla yeniyeni kapena inu simungakhulupirire izo. Nkulondola uko? Chotero iyo ikuyenera kukhala kutsanzira kwabwino kwenikweni.

¹⁴⁹ Ndipo ngati Yesu anati mizimu iwiriyo mu masiku otsiriza ikanadzakhala yoyandikana kwambiri mpaka ikanadzakhoza kudzanyenga Osankhidwa ngati nkotheke, anthu achipembedzo. Tsopano kumbikirani. Tsopano, palibepo kalikonse kunjwa uko mu zakalezo zo...zo...zozizira, zofunda. Kunjako iwo angokhala ndi maonekedwe a umulungu, inu mwaona. Koma mizimu iwiri iyi, mizimu yeniyeni, ikanadzakhala yofanana kwambiri mpaka iyo ikanadzakhoza kunyenga Osankhidwa omwe, mmene iyo ikanadzamagwirira ntchito mbali ndi mbali mmasiku otsiriza. Kodi Yesu ananena zimenezo? Iye anatero.

¹⁵⁰ Tsopano penyani, abwenzi, ine ndikujambulirani inu chithunzi chaching’ono. Ine ndikufuna kuti inu muyang’ane apa kwa miniti yokha. Ndipo mundipatsa ine tcheru chanu chosagawanika, chifukwa ine ndikupatsani inu fanizo, ndipo kenako inu muwona izo.

¹⁵¹ Tsopano, mu *Reader’s Digest*, zinalembedwa mmenemo, Ine ndinali nditaima kunjwa uko, ife tinali ndi anthu twente seveni handiredi akudikirira kuti apemphereredwe, ataima kunjwa uko. Inu munawerenga nkhaniyo. Ndipo mwamuna wina anabwera kuchokera ku Canada, ndipo iye anali ndi mnyamata wamng’ono amene anapita kwa a Mayos’ ndi John Hopkins, nthenda yovuta ya ubongo inakokera manja ake aang’ono mkati monga *chonchi*, ndipo inakokera miyendo yake pansi pake. Ndipo iwo anati, “Palibepo opareshoni kapena chirichonse chimene chingachitike.”

¹⁵² Chotero iye anamutengera iye kubwerera ku Canada. Iye anati, “Ine sindinakwapulidwebe.” Inu mukapeze ya *Reader’s Digest* ya mu Novembara, ndipo iyo imatchedwa a—a—*Chozizwa cha Donny Morton*. Ndipo—ndiyeno ananena kuti, mmenemo, kuti—kuti mwamunayo anati, “Ine sindinakwapulidwebe, chifukwa ine ndikumudziwa wochiritsa wa chikhulupiriro wotchedwa William Branham, zimenezo zinapangitsa awiri a azimzanga amene anali ogontha ndi osatha kuyankhula ndi kumva.”

¹⁵³ Ndipo iwo anayimba kuti ayesere kupeza kumene ine ndinali, mu—mu Amerika komabe. Ndipo ine ndinali ndiri ku Costa Mesa, California. Ndipo iyo ndi nkhani, inu mukawerenga iyo, inu mukakonzekere kuti mukalira. Iyo ingangokuswani

mtima. Mmene iye anadutsira mu zidikha za chisanu, ndi china chirichonse, ndi mwana ameneyo! Iye anati, “Usamale, Donny.” Anati, “Tsopano, ife si ogonjetsedwa.” Ndipo mnyamatayo sankamwetulira konse, nkomwe, iye anali atasautsika kwambiri. Anati, “Ife sitinagonjetsedwe, ife tikamufunsa Mulungu. Ife tipita kwa mneneri wa Mulungu ndipo tikamufunsa iye.”

¹⁵⁴ Chotero ndiye iwo anabwera kudutsa mu chisanu. Ndipo potsiriza iwo anakafika kumeneko, ndipo amayi anali akubwera ndi iwo, ndipo iwo analibe ndalama zokwanira zopitira pa ndege, chotero iwo anawabweza amayiwo. Ndipo mnyamatayo ndi abambo anabwera pa basi, ndipo mmene iwo anakwerera kuchokera komwe ku Winnipeg, Canada, kupita ku Costa Mesa, California. Ndipo iwo anakafika kumeneko, oshota, ndipo abambo akukamba za kumusinthwa iye matewera, mnyamata wamng’ono wa pafupifupi usinkhu wa zaka seveni kapena eyiti zakubadwa, basi wosowa thandizo kwenikweni. Ndipo momwe iye anka...sankapeza mwayi woti adye kapena chirichonse, ndipo anati mnyamata wake wamng’ono ankangomumva iye akamayankhula. Ndipo iye ankadziwira mmene maso ake ankawonekera, kuti iye anka—iye anali kuyesetsa kuti amwetulire, inu mukudziwa. Ndipo ankadziwa kuti iye...Iye akanakhoza kumuuzwa iye zochitika zosiyanasiyana zimene iye ankaziwona, uko mu Amerika.

¹⁵⁵ Ndipo pamene iwo anakafika kumeneko, ku California, iwo ananena kwa othandizira apaulendo, zimene iwo anabwerera kudzaziwona. Iye anati, “Mwabwera kudzamuwona Wauzimu wanji?” Ndipo chofunsira chachikulu.

¹⁵⁶ Ndithudi, inu mukhoza kulingalira chimene Amerika ananena za izo, inu mwaona. Mwaona, ndi ifeyo, mwaona, “Ife ndi anzeru kwambiri! Ife timadziwa chirichonse, inu mukudziwa, ndipo palibepo chifukwa chotiuzira ife chirichonse. Ife tazilemba zonsezo.” Mukuona?

¹⁵⁷ Chotero ndiye, chotero, “Chauzimu chiyani? Mwabwera njira yonse kuchokera ku Winnipeg, Canada?” Bwanji, iwo ankaganiza izo zinali zowopsya.

¹⁵⁸ Mulimonse, a nyuzipepala anakonza a—galimoto ndipo anamutumiza iye kumeneko. Ndipo iye anati, pamene iwo anadzafika pa mzere, kumene iwo unali, anati anthu twente seveni handiredi anali akudikirira kuti apemphereredwe. Koma anati, pamene iwo anamuwona mnyamata wolumala ameneyo, wooneka wamng’ono, ndi bambo wosauka atavala chipewa, chikhothi chake chakutha, anati aliyense anangoyima pambali ndi kumupatsa iye malo ake. Pamene iye anadzafika pa nsanja... .

¹⁵⁹ Izo ndi zotsutsana malamulo kusinthanitsa khadi la pemphero. Winawake akuyenera kubwera ku msonkhano ndi kudzatenga khadi lanu. Ngati inu mungapezeke konse pa mzere,

mukusinthana makadi a pemphero ndi winawake, khadi la pempherolo limakhala lopanda ntchito. Mukuona? Chifukwa inu mukuyenera kubwera kudzamva malangizo ndi kudziwa mmene mungalandirire iyo. Izo ziri kwa inu. Inu simungamulandirire iyo winawake. Inu mukuyenera kubwera ndi kudzatenga iyo nokha, kuti mudzamve. Munthu wina wamkulu anati, “Ngati . . . Chabwino, ine sindimakhulupirira mochuluka mu chinthu ichi. Koma, mwinamwake ngati Iye angandichiritse ine, ine . . .” Inu mukuona? Ndiyeno zimenezo zimayambitsa mikangano pa nsanja, chotero iwo amangochichotsapo chinthu chimenecho icho chisanafike kumeneko.

¹⁶⁰ Chotero pamene mnyamatayo anayamba, kapena abambo anapita pa nsanja, patsogolo pa anthu, Billy anamufunsa iye khadi la pemphero lake. Iye analibe lirilonse. Anati, “Ndiye ine ndikupepesa, bwana.” Anati, “Inu mukuyenera mudikire.”

¹⁶¹ Iye anati, “Chabwino.” Anati, “Ine ndidikirira.” Anati, “Ine nditenga nthawi yanga ngati enawa, ndiye.” Anati, “Ine sindimadziwa kuti ndimayenera kuchita ichi.”

¹⁶² Ndipo chotero ine ndinkayankhula ndi winawake, zinachitika kuti ndinamva izo. Ine ndinawawona abambo amenewo akuchokapo, ndipo ine ndinati, “Vuto linali chiyani?”

Iye anati, “Iye analibe khadi la pemphero.”

Ndipo Chinachake chinati kwa ine, “Mubwezeni iye.”

¹⁶³ Chotero ine ndinati, “Mubweretseni iye pano.” Ndipo abambowo anabwera, ndipo misonzi ikuyenderera pa masaya awo, akusowa kumeta. Ndipo iye—iye anayenda chokwera, ndipo apa *Reader's Digest* inatero. Mukuona? Ine sindinafunse mafunso, koma ndinayang'ana molunjika mmaso mwa mwanayo, ndinamuuza mwanayo kumene iye akuchokera, iye anali atapita ku Chipatala cha a Mayos, ndi zonse zimene zinali vuto ndi iye, mmene iye anadwalira, ndi chirichonse.

¹⁶⁴ Ndipo chotero abambowo anayamba kulira, ndipo anayamba kuchokapo. Ndipo anati anayamba kuchoka pa nsanja, ndipo anatembenuka, iye anati, “Uko nkulondola, bwana.” Iye anati, “Koma mwana wanga akhala moyo?”

¹⁶⁵ Ine ndinati, “Zimenezo ine sindinganene.” Ine ndinati, “Mphindi chabe.” Ine ndawona masomphenya akuwonekera. Ine ndinati, “Inu simungafune kukhulupirira izi, chifukwa a Mayos ndi Hopkins onse awiri ananena kuti opareshoni singachitike mu ubongo umenewo, koma ine ndikuuzani inu choti muchite. Inu, mawa, inu mungopita ndi mwanayo. Mu masiku atatu otsatira mukakumana ndi mkazi wa mutu wakuda pa msewu, ndipo mkazi ameneyo akakufunsani inu chimene chamuvuta mwanayo. Ndipo kenako iye akakuuzani inu za dokotala wina wamng'ono wa kumidzi kunja kuno amene angapange opareshoni imeneyo, ndipo inu simukafuna kuti mukhulupirire zimenezo, chifukwa a Mayos anazikana izo ndipo anati, ‘Izo

zinali zosatheka kuti zichitike.’ Koma umenewo ndi mwayi wokhawo umene mwana wanu ali nawo, kudzera mu mphamvu ya Mulungu, chifundo cha Mulungu ndi oparesoni imeneyo. Tsopano, ngati inu mukundikhulupirira ine kukhala mneneri Wake, pitani mukachite mmene ine ndakuuzirani inu.” Ngati kuyika mkuyu pa Hezekiya, ndi zina zotero.

Iye anati, iye anatembenuka ndipo anati, “Zikomo inu.” Anachokapo.

¹⁶⁶ Masiku awiri kapena ochuluka anadutsa, ndipo iye anali kumusi pa msewu tsiku lina, ndipo dona anabwera, anati, “Vuto ndi chiyani ndi mwana wako?”

¹⁶⁷ Anati, “Iye ali ndi a—nthenda ya ubongo.” Ndipo iye anali akupitirira kuyankhula monga choncho. Ndipo, chabwino, iwo—iwo anaganiza izo zinali zoyipa kwambiri, inu mukudziwa.

¹⁶⁸ Chotero iye ananena kuti mu maminiti ochepa chinachake chichitika. Iye anati, “Bwana, ine ndikumudziwa winawake amene angachite oparesoni imeneyo.”

¹⁶⁹ Iye anati, “Dona, taonani, a Mayo Brothers anakanika izo ndipo anati izo sizingachitike.” Anati, “Mwamuna kumtunda uko amamupempherera iye, wotchedwa M’bale Branham.” Anati, “Iye anapereka pemphero pa mwanayo.” Iye anati, “Dikirani miniti! Wa mutu wakuda, atavala suti yotuwa.” Anati, “Ndi ameneyo.” Anati, “Dokotala ameneyo alikuti?” Ndipo donayo anamuza iye. Anamutengera iye kumeneko ndipo dokotalayo anapanga oparesoni, mwanayo anachira.

¹⁷⁰ Tsopano, zimenezo zinachokera mu *Reader’s Digest*, inu mwaona. Ndipo a Mayo Brothers anandiimbira ine pa zokambirana za zimenezo. Anati, “M’busa Branham, inu munachita chiyani kwa mwanayo?”

¹⁷¹ Ine ndinati, “Palibe. Ine sindinamugwire iye nkomwe. Ine ndinangonena chimene Mulungu anandiiza ine kuti ndimuze iye. Mwamunayo anamvera izo.”

¹⁷² Tsopano, chinthu chosangalatsa cha izo, pafupifupi masabata awiri izo zitachitika, kapena masabata awiri pambuyo pa zimenezo, kapena atatu, mu *Reader’s Digest*, mwina wake mwezi patsogolo, nkhanu ya Abiti Piper inatulukira. Tsopano, iye ndi mfiti yeniyeni, kapena wamatsenga. Tsopano, pali weniweni, ndipo pali wina wongotsanzira. Iwo akhala naye mkazi ameneyo kuyambira 1897. Iye ndi wausinkhu wopitirira zaka handiredi zakubadwa tsopano, mu New York, awiri onse... wogontha kwambiri. *Reader’s Digest*, inatenga... ine ndikuganiza iyo inatuluka pafupifupi miyezi iwiri kapena mwezi yanga isanatuluke; ndipo inu mukhoza kuyipeza iyo, kumayambiriro kwa chirimwe. Bambo Baxter anali nawo kuno tsiku lina. Ngati ine ndikanaganiza za izo, ine ndikanamutenga iye... kapena ndikanadziwa kuti ndinena izi, ine—ine ndikanaitenga iyo. Ine ndikhoza kukubweretserani

inu. Ndipo ili ndi masamba pafupifupi thwelofu kapena fortini. Iye anali mkazi wapanyumba chabe. Ndipo iye analowa mu chizimbwizimbwi tsiku lina, akuvutika, ndipo iye anayamba kuyankhulana ndi akufa. Ndipo iwo akhala naye mkazi ameneyo konsekonse pa dziko, paliponse. Iwo anamutengera iye ku England. Kumamusintha zovala zake kumene, nthawi zambiri, ndi kukawona ngati panali zolakwitsa ndi zinthu, ndipo anapita kumeneko ndipo anamuzimbaisa winawake ndi chigoba pa nkhope, Mgriki, ndipo nkumachia ngati waku England. Ndipo anamuuza iye zonse za izo. Ndipo iye—iye—iye ankafuna kuti aitane mmodzi wa abwenzi ake akufa.

¹⁷³ Tsopano, chinthu chokhacho chimene iye...Kuzungulira dziko lonse, ndipo apa *Reader's Digest* inanena pamene, kuno mausiku angapo apitawo, kapena miyezi ingapo yapitayo, chimodzi cha zinthu zimenezo chinayalusidwa. Mwamuna ankayenera kupsyopsyona dzanja la mzimu wa amayi ake, ndipo tsiku lotsatira izo zinatsimikiziridwa mu kothi la polisi kuti iye anangopsyopsyona chidutswa cha nsalu yopyapyala. Anthu ambiri akutsanzira wamatsenga! Pali owerenga akale awa amene amakhala mbali mwa msewu, amene si amatsenga kuyamba ndi kuyamba. Iwo si kanthu koma otsanzira akuba. Koma alipo wamatsenga weniweni.

¹⁷⁴ Ndipo ife anthu achipembedzo, ife tiri ndi otsanzira ochuluka mbali ziwiri zonse. Tsopano dikiriranibe kwa maminiti ochepa.

¹⁷⁵ Tsopano zindikirani, kuti Abiti Piper ndi wamatsenga weniweni. Ndipo magazini anati, “Apa pali chinthu chimodzi chimene chingatsimikiziridwe, kuti, munthu akafa, iye sanafe. Iye amakhala ali moyo kwinakwake, chifukwa mkazi ameneyo amawuitana mzimu wawo kubwera ndi kumayankhula ndi anthuwo.”

¹⁷⁶ “Tsopano, iye amachita chiyani, M'bale Branham? Kodi inu mukuzikhulupirira izo?” Inde, bwana. Baibulo limanena chomwecho, ndi chifukwa chake ine ndimazikhulupirira izo. Ndipo iye ndi wa mdierekezi. Zamizimu ndi njomba ya mdierekezi. Tsopano zindikirani, tsopano apenyeni awiriwo.

¹⁷⁷ Ndiyeno inu mukanati muwone makalata akubwera kwa ine, nthawi imeneyo, pamene nkhani yanga inatsatira yake. Kodi izo sizachirendo kuti, basi asanafike mapeto a nthawi, Mulungu anayankhula zinthu izi? Ndipo *Reader's Digest* imasindikizidwa mu chinenero chirichonse pansu pa thambo. Mukuona? Zindikirani, kodi izo si zachirendo kuti izo zinatsatana ina ndi imzake?

¹⁷⁸ Tsopano apa panabwera makalata, anati, “M'bale Branham, zimenezo zikutsimikizira kuti inu si kanthu koma wamatsenga.” Anati, “Izo zikutsimikizira izo. Tayang'anani apa, inu

munamuza mkazi uja kumene ati akapeze. . . Muoneni mkazi *uyu?*”

¹⁷⁹ Ine ndinati, “Dikirani miniti.” Ine ndinatulutsa kalata yovomerezeka, (mundikhulukire ine), kuti nditumize kwa anthu. Ine ndinati, “Alaliki inu mumadziwa zochepa bwanji.” Ine ndinati, “Mmalobabatiza thupi lanu, inu mukusowa kubatiza ubongo wanu.” Uko nkulondola. “Inu simusiya kuganizira zinthu. Inu simuyesera kuziganizira izo.”

¹⁸⁰ Ndiyo njira yomweyo imene iwo ankachitira mmasiku enawo. Iwo anamuwona Yesu. Iwo anadziwa kuti Iye akanatha. . . Iye ankadziwa zinsinsi za mu mtima mwawo. Iye ankadziwa zimene iwo ankachita monga choncho. Ndipo iwo anati, “Iye ndi wamkulu wa adierekezi. Iye ndi Bezebule, wambwebwe wapamwamba kwambiri mdzikoli.” Iwo sanayime kuti ayesere kuziganizira izo, kuti awone kuti ameneyo anali Mwana wa Mulungu. Iwo sanali auzimu mokwanira kuti adziwe izo. Ndi zimenezotu, iwo anawerenga pamwamba pa chinthucho. Ndithudi, Yesu ankayenera kubwera mu Yerusalemu, atakwera bulu, ndi zina zotero, koma iwo ankayang’ana pa Kudza kwachiwiri.

¹⁸¹ Ndipo chinthu chomwecho lero! Iwo akuyang’ana pamwamba pa chinthu chenichenicho. Aleluya! Uko nkulondola. Ine ndikudziwa kuti Mulungu ali pano, masana ano, ndipo ine ndikudziwa ndikutenga nthawi yanu yochuluka, koma inu mukuyenera kuchiwona ichi, mzanga. Ngati ine sindidzakuwonaninso inu, inu mukuyenera kudziwa chimene ziwanda ziri, inu mukuyenera kudziwa chimene Choonadi ndi cholakwika chiri. Ndipo izo ndi zoyandikana kwambiri, inu mukuyenera kulekanitsa chinthucho.

¹⁸² Tsopano kumbukirani, izo sizidzakhala kunja uko, chinachake uko mbali *iyi* ngati Afarisi, kapena chinachake mmbuyo kumbali *iyi*. Icho chiri pomwe apa pakhomo, pafupi ndi icho. Penyani icho. Tsopano ngati ine ndinatenga. . .

¹⁸³ Tiyeni titenge nkhani ziwiri zimenezo. Ngati ine nditatenga ndi kukupatsani inu dolla, tsopano, ngati ine nditakupatsani inu dolla yabodza. Ife tigwiritsa ntchito fanizo kuti mumvetse. Chinthu choyambirira chimene inu mungapange, ngati inu muli munthu wanzeru, ngati inu mungatenge dolla ndi kuiyang’ana iyo, chinthu choyambirira, inu muikhudza iyo ndi kuiwona chimene iyo inapangidwira. Nkulondola uko? Inu mudzayang’ana chimene iyo inapangidwira. Inu mudzayang’ana pa mtengo wake. Dolla yeniyeni siimapangidwa kuchokera ku pepala, gawo lina ndi pepala ndi silika, inu mwaona. Ndipo chinthu choyambirira, inu mudzayenera kuyang’ana pa mtengo wake. Chimenecho ndicho chisonyezero choyamba.

¹⁸⁴ Ndipo tsopano tiyeni timutengere iye uko mbali *iyi*; ndipo tiwatengere Ambuye mbali *iyi*, amene akuchita ndi ife.

185 Tsopano taonani, chinthu choyambirira chimene inu mukuyenera kuchizindikira, chirichonse. . . Yang'anani nkhani yanuyo. Mu zaka fifite-chakuti zosamvesetseka zake za mbwebwe, ndi kuyitanira mizimu ya akufa, iye sanamutchulepo nkamodzi komwe Mulungu, Khristu, machiritso Auzimu, chiombolo, Chiweruzo, kapena chirichonse. Palibepo kalikonse koma kusangalala ndi kupusitsa mmenemo.

186 Koma uko kumbali *iyi*, izo ndi mopitirira Mulungu, Chiweruzo, Kubwera kwa Yesu, machiritso Auzimu, mphamvu ya Mulungu, chiwombolo. Tayang'anani pa kufunikira kwa izo. Inu simumawawona ambwebwe ndi afiti ali kunja akulalikira Uthenga. Vuto ndi chiyani ndi anthu? Mai! Zindikirani!

187 Ndipo chinthu chenicheni choti muchite, ngati mukufuna kudziwa ngati ili dola yeniyeni kapena ayi, ngati ikuwoneka kwambiri monga iyo, chotsanipo manambala ndi kuitumiza iyo kopanga ndalama. Ndipo ngati pali manambala pamenezo omwe akufanana ndi iyo, pali dolla ya siliva yomwe ikudikirira iyo. Nkulondola uko?

188 Chabwino, ndiye, m'bale, tengani chimene iye anachita ndi kuchibwezera icho ku Baibulo, inu mudzapeza kuti ndi mfiti ya ku En-dori.

189 Ndipo inu mutenge chimene chiri pano, mukachipeza icho mmbuyo, chiri pa Bukhu apa mu Chikombole, "Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse." Ndithudi, ntchito Yake yomweyo! Iye sanapite ndi kupusitsa ndi zamkutu ndi anthu. Izo zinali za ubwino wina, kuti zithandize winawake, kuti ziwatsogolere iwo kwa Mulungu. Amen! Ine sindikudzinenera ndekha "ameni", koma *ameni* amatanthauza "zikhale chomwecho." Ndipo ine. . . ine ndikuzikhulupirira Zimenezo. Ine ndikudziwa Icho ndi Choonadi.

190 Tsopano zindikirani, ndi inu apa. Tsopano, mofulumira tsopano, chifukwa ine sindikufuna ndikusungeni inu motalika.

191 Apa, tiyeni tipereke chithunzi chaching'ono apa, chithunzi chaching'ono cha mmalingaliro. Apa pali mtsinje womwe ukudutsa apa, kutsika kudutsa njira *iyi*, ukubwera chotsika kudutsa mmoyo. Tsopano penyani. Iwo ndi mpita. Ndipatseni ine tcheru chanu chosagawanika tsopano, kuti musaphonye izi. Pansi pomwe monga *chonchi*. Tsopano, mu kampita kakang'ono aka apa mumakhala anthu achivundi, inu ndi ine. Tsopano, mmenemo, tiyeni tiwone chomwe icho chiri. Ndi mulu wa zopusa ndi china chirichonse, koma kamodzi pa kanthawi inu mumawona kuwala. Mukuwona mdima ndi misewu, ndizo zosangalatsa ndi kumangopitirira, ziwanda kuwagwira anthu. Oh, iwo amavala bwino, mai, ndipo otukuka kwambiri momwe iwo angakhalire, masikolala opukutidwa, komabe mdierekezi. Koma pali obadwa mwatsopano akukhala pamenezo.

192 Tsopano, anthu awa mu mpita uwu amakopedwa kuchokera mbali ziwiri zosiyana. Tsopano, kumbali iyi kupita mbali *iyi*, kuli utatu. Ndipo mbali iyi kupita mbali *iyi*, kuli utatu.

193 Tsopano, pamene, tsopano malo oyambirira, mbali *iyi*, ndi miyoyo ya *osalungama*, munthu akafa amapita kumalo oyembekezera chiweruzo. Yesu anapita ndipo anakalalikira kwa miyoyo yomwe inali m'ndende kumeneko. Otsatirawo ndi ziwanda. Otsatirawo, ndi mdierekezi ku gehena. Kumapita chokweza, woyamba, tsopano, iwo amene ali mmenemo ndi mizukwa, mizima ya anthu akufa amene sanalape. Iwo akuyembekezera Chiweruzo. Chithu chokhacho chimene iwo akuchidziwa ndi kupusa ndi zomwe iwo anachita.

194 Tsopano, kumtunda kuno, Akhristu awa amakopedwa kuchokera Kumwamba. Ili ndi fanizo. Pamwamba apa pali Mzimu wina, Mzimu Woyera, Mzimu wa Munthu, Khristu Yesu. Mzimu Woyera, Mzimu Woyera umawukopa Mpingo Wake mu dera lachivundi ili.

195 Mdierekezi, ndi mizimu *iyi*, amamukopa munthu. Tsopano, penyani, chotsatira ndi Angelo. Wotsatira ndi Mulungu. Tsopano, wachivundi aliyense pano amakopedwa ndi limodzi la maiko awa. Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza?

196 Tsopano chimene mkazi ameneyo anachita, iye anakalowa mu dera limenelo. Ndipo iye akuyankhula ndi amuna odzazidwa ndi ziwanda amene anali, poyambirira, mizimu ya angelo akugwa amenewo amene sanalape kumbuyo pachiyambi, ndipo analola matupi awo kuti adzazidwe ndi izo. Ndipo iwo akuyembekezera Chiweruzo.

197 Ndipo *awa* kuno amakopedwa ndipo anabadwanso kachiwiri ndi Mzimu wa Mulungu. Ndipo mdierekezi ali nawo aneneri ake, ndipo Mulungu ali nawo Ake. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Ndi chikoka, ndipo apo ife tikupita. Taimikira kuti tilekanitse izo. Yesu, pamene Iye anali kuno padziko lapansi. . .

198 Tsopano, lero, iye sangakhoze kukalowa mu dera limenelo ndi kukatengako munthu wolungama kuchokera mu gawo limenelo. Iye sangakhoze kuchita zimenezo, chifukwa amuna olungama kulibeko kumeneko kumene iwo ankakhalako, mu Paradiso. Ayi, bwana. Paradiso anathetsedwa, pamene Magazi a Yesu anachotsapo iye. Yang'anani apa. Mai!

199 Ngati ine ndingaganizire za momwe Yesu, pamene Iye anafa, Iye anapita ndipo anakalalikira kwa masolo amene anali m'ndende. Iye anafa, wochimwa, asakudziwa tchimo, komabe tchimo lathu linali pa Iye. Ndipo Mulungu, chifukwa cha machimo Ake, anamutumiza Iye ku gehena. Baibulo linati, "Iye anapita ndipo anakalalikira kwa miyoyo."

200 Anthu ena amati, "M'bale Branham, ine sindikutha kuzimvetisa izo." Anati, "Yesu anauka pa tsiku lachitatu.

Anamwalira Lachisanu masana ndipo anauka Lamlungu mmawa, bwanji, Iye anangofa tsiku limodzi.”

²⁰¹ Iye anati, “Mkati mwa nthawi zimenezo,” pakuti Iye anali ndi Lemba limodzi mu Baibulo, limene Iye akanaimapo. Pakuti, Davide, munthu amene anali atabwerera mmbuyo patsogolo pake, koma iye anapulumsidwa, koma mneneri pansi pa kudzoza kwa Mulungu, anati, “Ine sindidzasiya moyo Wake mu gehena, komanso sindidzalola Woyera Wanga kuti awone chivundi.” Ndipo iye ankadziwa, masiku atatu ndi usiku, kuti thupi limenero likanakhala mu chivundi. Ndipo Mulungu anali atapani kale kwa mneneri, “Sadzawona chivundi.” . . .? . . . [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi].

Aleluya! Iye anatenga Mawu a Mulungu. Iye anamugonjetsa Satana, nthawi iliyonse, pa Iwo. Iye anagonjetsa imfa, pa Mawu a Mulungu. Aleluya! Iye anagonjetsa imfa. Ndipo pamene iwo anamupha Iye, ndipo Iye anafa, wochimwa, machimo anga ndi machimo anu pa Iye, Iye anapita pansi, Ine ndikukhoza kumuwona Iye akugogoda pa khomo limenero pamenepo.

Ndipo miyoyo yotayika iyo inatulukira ndikuti, “Chabwino, Inu ndi Ndani?”

²⁰² Iye anati, “Nchifukwa chiyani inu simunamumvere Enoki? Nchifukwa chiyani inu simunawamvere aneneri ena omwe ankalalikira?” Iwo anaweruzidwa. “Ndine Mwana wa Mulungu amene anakhalapo ndi moyo. Ine . . . Magazi Anga akhetsedwa. Ine ndabwera kudzakuzani inu, Ine ndakwaniritsa, zimene aneneri ananena kuti Ine ndidzachita.” Anali akutsikira mmusi kudutsa ziwanda, mpaka ku gehena, anakatenga mafungulo a imfa ndi gehena kumulanda mdierekezi, anawapachika iwo pa mbali Yake, anayamba kubwerera. Aleluya!

²⁰³ Analawirira mmawa. Aleluya! Tiyeni tijambule chithunzi chaching’ono apa. Mmawa kwambiri, kuli gulu lina limene likugona kuno mu Paradiso. Iwo kulibeko uko tsopano.

²⁰⁴ Tsopano, inu abwenzi aakulu Achikatolika omwe mumakhulupirira mu kupembedzera kwa oyera. Ngati inu mukuyankhula ndi woyera mu mpingo wanu, mwamuna ameneyo ndi wochimwa, iye ali ku gehena, kapena—kapena akuyembekezera chiweruzo chake uko. Ndipo ngati anali woyera, iye ali mu ulemmero wa Mulungu ndipo sangabwererense. Uko nkulondola. Ine ndikhoza kutsimikizira zimenezo. Magazi a ng’ombe sakanachotsa tchimo, koma Magazi a Yesu anasudzula machimo.

²⁰⁵ Ine ndikukhoza kumuwona Yesu akupita uko kumene, Paradiso, kuli Abrahamu wakale, Isaki ndi Yakobo, ndi iwo mmenemo, Samuele ndi ena onse a iwo mmenemo. Ndikumumva Iye akugogoda pakhomo. [M’bale Branham agogoda paguwa ka sikisi—Mkonzi]. Ameni! Oh, ine ndikuzikonda izi. Ine ndikufika pomwepo . . . ndikumverera ngati wachipembedzo tsopano. Ine

ndikukhoza kumuwona Iye akuyang'ana cha uko. Ndikumumva Iye akuti, “Ndani ali kunja uko? Ndi Ndani kumeneko?” Iye anati, “Ine, uyu ndi Abrahamu akuyankhula. Kodi ndi Ndani?”

²⁰⁶ “Ndine Mbewu ya Abrahamu.” Ameni. Ine ndikukhoza kumuwona Abrahamu akubwera pakhomo, kudzatsegula chitseko. Iye anati, “Ndine Mbewu ya Abrahamu.”

Daniele anati, “Taonani pamenepo! Apo pali Mwala umene ine ndinawuwona ukusemedwa kuchokera m'phiri.”

²⁰⁷ Ine ndikukhoza kumumva Ezekieli akuti, “Ndi Uyo apo! Ine ndinamuwonapo Iye, munga fumbi pansi pa mapazi Ake, mitambo ikuyenda, pamene nkhosa . . . anawomba mmanja mwawo, masamba, ndipo onse anafuula.” Oh, ine ndikuwawona osiyanasiyana kumeneko mu Paradiso, akumuyembekezera Iye.

²⁰⁸ Ine ndikukhoza kumumva Iye akuti, “Kazibwerani! Kukuyamba kucha uko ku Yerusalemu. Ife tikuyenera kuti tichokeko kuno. Ife tikupita mmwamba, chifukwa inu munadalira mmagazi a ng'ombe zamphongo ndi mbuzi, mu kudikirira nthawi ya Magazi Anga. Koma Magazi Anga akhetsedwa kumtunda uko pa Kalvare. Ndine Mwana wa Mulungu mthupi. Ngongole zonse za tchimo zalipiridwa. Ife tiri pa ulendo wathu wotuluka!” Aleluya! Ulemelero kwa Mulungu!

²⁰⁹ Ine ndikukhoza kumuwona Abrahamu atamugwira Sarah pa nkono, ndipo apa iwo akubwera, akutuluka! Mu Mateyu 27, pamene iye ankatuluka, Ine ndikukhoza kuwamva iwo ataima pang'ono ku Yerusalemu uko. Ndipo chinthu choyambirira inu mukuchidziwa, Ine ndikukhoza kumuwona Kayafa ndi iwo ataima pa msewu, akuti, “Iwo akundiwuzwa ine kuti munthu uja wauka. Akuti, munthu ameneyo ndi ndani amene akupita kumeneko; mnyamata wamng'ono uja, mtsikana wamng'ono uyo?”

²¹⁰ Osati wokalambanso panonso; ameneyo anali Abrahamu ndi Sarah. Ndipo iwo anasowa. Iwo anayang'ana, “Winawake akutiwona ife.” Iwo amatha kusowa momwe Iye ankadutsira pakhoma, mtundu womwewo wa thupi. Aleluya! Kulondola. Apa pali aneneri onse ndi iwo, akuyendayenda, akuyang'anayang'ana mzindawo.

²¹¹ Ndipo Yesu anatsogolera kukalowa mmwamba, kapena pamwamba pa nyenyezi, mwezi, mitambo, ndipo anatsogolera amsinga ku undende, anapereka mphatso kwa anthu. Yesu akukhala lero kudzanja lamanja la Atate, anakwera pamwamba apo, anakakhala pansi, mpaka adani Ake onse atakhala choponderapo mapazi Chake.

²¹² Ndipo lero, mzanga wokonedwa Wachikhristu, ziwanda zikugwira ntchito paliponse. Ndipo Mzimu wa Mulungu ukusuntha, kumbali inayo, kuti ukamenyane ndi iwo nthawi iliyonse. Aleluya! Ndi zimenezotu. Manyuzipepala ndi digests ndi zina zonse akulengeza izi. Iwo akuzipenya izi. Iwo

akulephera kuwona chomwe izo ziri. Icho ndi chiyani? Ndi chithunzi cha chiwonetsero chachikulu chimene chikubwera posachedwapa, pakati pa Mulungu ndi mdierekezi. Khalani kumbali ya Mulungu ndipo mukhale owona mu mtima mwanu. Amen.

²¹³ Kuno osati kale kwambiri ine ndinali ku Toledo, Ohio, ndinali ndi msonkhano. Ine ndikutseka.

²¹⁴ Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza zokhudza ziwanda? Izo zikugwira ntchito. Izo ndi zachipembedzo kwambiri, zachipembedzo basi! Oh, izo zimapita kutchalitchi Lamlungu lililonse, zimabwereza Kachikhulupiro ka Atumwi, ndi kuimba Matamando. Oh, mai, zachipembedzo basi momwe izo zingakhali!

“M’bale Branham, inu mukutanthauza kuti icho ndi Choonadi?”

²¹⁵ Ndiwo mtundu wa mzimu umene unamupachika Yesu Khristu pa mtanda. Ndipo Yesu anati, “Ndinu a atate anu, mdierekezi.”

²¹⁶ Tsopano ena a iwo anati, “Oh, Russia ndi wotsutsakhristu.” Osatheka! Russia si wotsutsakhristu. Wotsutsakhristu adzakhala wachipembedzo kwambiri izo zidzapusitsa Osankhidwa kumene ngati kukanakhala kotheka.

Kumbukirani, Mulungu amamutengapo munthu Wake, koma osati Mzimu Wake. Mdierekezi amatengapo munthu wake, koma osati mzimu wake. Tsopano, ndi iwo pamene. Dzifanizitseni nokha. Ine ndimangoyankhira Choonadi.

²¹⁷ Ziwanda, zikugwira ntchito! Dzulo, ndinali nazo izo mu dera lathupi. Lero, ine ndikukuwonetsani inu mu dera lauzimu, pamene izo ziri mu dera lachipembedzo. Kumene izo ziri kutali uko, zotchedwa khansa, ndipo iwo amazitcha *ichi*, *icho*, ndi *chimzake*, koma ine ndatsimikizira kwa inu, mwa Baibulo, izo ndi ziwanda. Tsopano, apa, lero, apa izo zirinso mu dera lachipembedzo, zachipembedzo kwambiri, zodzipereka kwambiri.

²¹⁸ Ngati inu mungayambe, m’bale, ndikuganiza. Kaini, chiyambi chake chomwe, anali munthu wachipembedzo kwambiri. Esau anali munthu wachipembedzo kwambiri. Yudasi anali munthu wachipembedzo kwambiri. Ndi chipembedzo. Si dziko lakunja. Ndi momwemo mu maudindo. Penyani izo, phunziro la ziwanda! Mwinamwake mtsogolo pang’ono, nthawiyina, ine ndikhoza kudzafika pa izo mopitirira pang’ono. Ife tikuchedwa.

²¹⁹ Osamuweruza aliyense. Kondani aliyense. Ngati inu simungakonde kuchokera mumtima mwanu, ndiye kuti Khristu sali ndi inu.

220 Ku Toledo, Ohio, ine ndinapita mu malo odyera aang’ono. Ine ndakhala ndikudya pa malo, malo aang’ono a Dunkard, malo aang’ono abwino. Iwo anali abwino kwambiri. Masana amenewo iwo anali atatseka, kuti apite ku Sande sukulu. Ndipo pamene iwo anatero, ine ndimayenera kupita kutsidya kwa msewu, kupita ku malo akale aang’ono achidziko, ndipo ine ndinakalowa mmenemo. Ndipo ine ndikudziwa kuti ndi zoletsedwa kutchova njuga ku Ohio. Ndipo apa panaima wa polisi wa deralo atayika nkono wake mokumbatira mtsikana, dzanja lake litamugwira iye apa pa chifuwa chake, akusewera makina a njuga. Lamulo la madera athu ndi dziko, zonse zapita. Zomvetsa chisoni!

221 Ine ndikudalira pa Khristu Thanthwe lolimba, ine ndaimapo, malo ena onse ndi mchenga wotitimira. Palibe chimene chatsalira. Uko nkulondola.

222 Ine ndinayang’ana kumbuyo uko, ndipo uko kunali dona wamng’ono wokongola, mwinamwake mu usinkhu wa mmatini ake, usinkhu wa zaka naintini, eyitini, naintini. Ndipo zimene iwo anali kuchita, anyamata amenewo kumbuyo uko pa tebulo, zinali zoyipa. Ine ndinakhala pansi pamenepo. Ndipo tsopano mwakudabwitsidwa kwanga, nditakhala pomwe apa pamene dona anabwera, anati, “Kodi inu mungakhale pampando?”

Ine ndinati, “Zikomo. Ine ndimafuna kadzutsa.”

223 Ndipo nditakhala pampando, apa panakhala dona wachikulire, wamkulu ngati amayi anga, usinkhu wa zaka fifite faifi, fifite eyiti zakubadwa. Iye anali atavala zovala zazing’ono zopanda umulungu izo zimene iwo amavala.

224 Iwo amati ndizabwino. Sayansi imati, “Ndiwe wamisala.” Ndithudi, sichoncho. Ukungofuna kuwonetsa umaliseche wako. Ndi zamanyazi, chitonzo. Dona sangavale zimenezo. Mkazi angatero, koma dona sangatero.

225 Ndiyeno, chotero ndiye iwo . . . iye anali pamenepo, atakhala pamenepo. Mnofu wake wosauka unali wolibwidika. Iye anali ndi mtundu wa zopaka zooneka ngati-maluwa, chirichonse chimene inu mumachitcha icho, pa milomo yake. Ndi kametedwe kakang’ono kwambiri ngati mwamuna, yemwe wasokonezeka yense; chimene Baibulo linanena, chimene chinali chamanyazi. Ndipo mkazi, amene mwamuna . . .

226 Baibulo limadzinenera, ngati mkazi adula tsitsi lake, mwamuna ali ndi ufulu womusiya iye banja, chifukwa iye siwoona mtima kwa iye. Iye tikuyenera titsike ndipo tilalikire Baibulo kuno limodzi la masiku awa. Linati, “Ngati iye akudula tsitsi lake, iye sakumulemekeza mwamuna wake.” Ngati iye ali wopanda ulemu, iye akuyenera kusiyidwa. Iwe sungakwatire wina, koma ukhoza kumusiya iye. Psyii! Mnyamata, izo, izo zikupita molimba, ine ndikukhoza kuzimverera izo. Koma ndicho Choonadi.

227 Oh, zinkakhala kuti, ife tinkakhala nazo mmagawo a Mzimu Woyera, koma tinalekelera zigwiriro. M'bale wachikulire anakonda kunena kuti, "Talekerera zigwiriro, ife talekerera zigwiriro, talinyengerera tchimo. Ife talekerera zigwiriro, nkhosa zinatuluka, koma mbuzi zalowamo bwanji?" Mwalekerera zigwiriro. Ndiro limene linali vuto. Mwasiya zigwiriro, dziko lapansi ndi mpingo zasakanikirana. Chimodzimidzi monga Amoabu ndi ena otero, ndi Balamu, ndi momwe iye anakwatirira pakati pawo, ndizo ndendende basi chinthu chomwecho lero. Ndipo mpingo wonse waipitsidwa, ndipo m'badwo wa Chipentekoste ndi m'badwo wa Laodikaya, umene ukufunda, ndipo walavulidwa kuchokera mkamwa mwa Mulungu. Ndipo kuchokera pagulu lonselo, Mulungu akuyitana otsalira Ake, akumutengera Iye Kwawo, ndiko kulondola ndendende, ndendende, kudutsa mu chiukitsiro.

228 Ndipo pamenepo iye anali, atakhala pamenepo, zopaka mmilomo ziri pa nkhope yake yonse, ndipo izo zinali paliponse monga choncho. Ndipo iye anali ndi ichi apa zinthu zakuda mmaso ake, ndipo iye anali akuchita thukuta, ilo linali likutsikira mmusi. Ndipo munthu wokalamba wosauka mwina anali ndi zidzukulutudzi. Ndipo iye anali atakhala pamenepo ndi amuna aakulu awiri, ndipo mmodzi wa iwo anali ndi mpango pakhosi lake, ndipo izo mu Juni, atakhala pamenepo. Ndipo iye anadzuka, ndipo amakhala ngati amamwa mowa, ndipo iye amamwa, nayenso. Ndipo iye anali akuyang'ana yang'ana.

229 Ine ndinaganiza, "O Mulungu! Mulungu, bwanji Inu simukungochichotsapo chinthucho pa mapu? Bwanji Inu simukutero? Kodi Sharon wanga mwamng'ono. . . Mwana wanga wamng'ono, Sarah wanga wamng'ono ndi Rebekah wanga wamng'ono akuyenera kukula mu m'badwo umenewo, kuti adzabwere ndi kudzakumana ndi zinthu ngati zimenezo?" Ine ndinaganiza, "Kuyang'ana kunja kuno mu mabwalo awa ndi zinthu, ndi zimene zimachitika." Ine ndinaganiza, "O Mulungu! Oh, ndine wokondwa Inu munamutenga Sharon ngati icho chinali chifuniro Chanu. Kodi Rebekah wanga wamng'ono ndi wamng'ono—Sarah wamng'ono akuyenera kuti adzaleredwe pansu pa zinthu ngati zimenezo?" Chimene, ndipo anthu amenewo amawatchula iwo. . . amaimba mu kwaya ndi chirichonse. Ndipo ine ndinaganiza, "Icho si chamanyazi?" Ine ndinaganiza, "Mulungu, chirungamo Chanu Choyera chingapirire nazo bwanji izo? Zikuwoneka ngati kuti mkwiyo Wanu worungama ungaulukire kumeneko ndi—ndi kudzaphulitsa malowa."

230 Ndipo ine ndinamumva Mngelo wa Ambuye, anati, "Bwera pambali." Ine ndinapita pamenepo. Ndipo pamene Iye anathana ndi ine, ine ndinamverera ngati munthu wosinthika. "Iwe ukumuweruziranji iye?"

Ine ndinati, “Tayang’anani izo, mmene iye aliri.” Ndipo apa pali chimene Iye. . .

²³¹ Ine ndinawona masomphenya. Ine ndinawona dziko ngati *ili*, lozungulira, dziko lina. Koma dziko ili *apa*, ilo linali ndi utawaleza molizungulira ilo, ndipo amenewo anali Magazi a Khristu amene amatetezera mkwiyo wa Mulungu. Iye sakanayang’ana pa ilo, Iye—Iye akanachiwongga chinthucho pompano, chifukwa Iye anati, “Tsiku limene mudzadya izo, tsiku limenelo mudzafa.” Chotero Iye akanachita izo.

²³² Kenako ine ndinaganiza chotere. Ine ndinadziwona ndekha. Ngakhale ine sindinachite izo, koma ine ndinali wochimwa, mulimonse. Ndiyeno Magazi a Yesu Khristu amachita kwa ife ngati bampara. Mukuona? Kuti, pamene ine ndichimwa, machimo anga amamunya Iye ndipo amavulaza mutu Wake wofunika, ndipo ine ndimakhoza kuwona misonzi ndi Magazi akutsikira pansi. “Mukhululukireni iye, Atate, iye sakudziwa chimene iye akuchita.” Ndipo ine nkuchita china chakenso ndipo nkumanya Iwo. “Mukhululukireni iye, Atate.”

²³³ Ngati izo zikanati zimudutse Iye, ine ndikanawonongedwa. Ndipo ngati ine ndikanati ndisalandire chisomo Chake, ndipo tsiku limene solo yanga idzayandame pamwamba pa izo, ine ndaweruzidwa kale. Ine ndakana. Palibepo chimene chatsalira koma chiweruzo. Kuweruzidwa, ine ndaweruzidwa kale. Mulungu anati, “Tsiku limene inu mudzadye za umenewo, tsiku limenelo inu mudzafa.” Inu mwaweruzidwa molondola. Uwu ndi mpando wachiweruzo masana ano, maonedwe anu pa Khristu.

²³⁴ Ndipo kenako ine ndinaganiza, “Inde, uko nkulondola.” Ndipo ine ndinawona tsiku lina ine ndinakwawira kwa Iye. Ine ndinawona bukhu langa lakale liri pamenepo, wochimwa, pamenepo panali chirichonse pa ilo. Ine ndinawona kuti machimo anga ndi amene anali kuchita zimenezo, ndipo ine ndinati, “Ambuye, Inu mundikhululukira ine?”

²³⁵ Anaika dzanja Lake kumbali Yake, anatulutsako Magazi ena, analemba pamwamba pake, ndipo anati, “Wakhululukidwa.” Analiponyera ilo kumbuyo uko mu nyanja ya kuyiwala, kuti asazakumbukire izo konse. Izo zinali zitapita kwanthawizonse! Iye anati, “Ine ndakukhululukira iwe, koma iwe ukumutsutsa iye.”

Izo zinasintha lingaliro langa. Ine ndinati, “Ambuye, ndichitireni chifundo.”

²³⁶ Ine nditatuluka mu zimenezo, ndinapita pamenepo ndipo ndinakakhala pansi. Ine ndinati, “Inu muli bwanji, amayi?”

Iye anati, “Oh, moni.”

²³⁷ Ndipo ine ndinati, “Ngati inu mungandikhululukire ine,” ine ndinati, “Ndine M’busa Branham, mtumiki.”

Iye anati, “Oh, pepani. Pepani, M’busa Branham.”

²³⁸ Ine ndinati, “Dona.” Ine ndinamuza iye nkhanio. Ine ndinati, “Ine ndinaima pamenepo, ndipo ine ndimakuweruza iwe, ndi kumaganiza, ‘Ndi chinthu choyipa bwanji!’ Mwinamwake iwe uli ndi ana.”

Iye anati, “Ine ndiri nawo.”

²³⁹ Ine ndinati, “Chinapangitsa njira kulakwika ndi chiyani?” Iye anayamba kufutukula nkhanio kwa ine imene ikanakhoza kung’amba mtima wa chirichonse. Ine ndinati, “Ine—ine ndimamupempha Mulungu chifukwa chiyani Iye sakungochotsa zoterozo pa dziko lapansi. Apa, iwe uli apa ndi amuna oledzera awiri awa, ndipo iwe waledzera, iwemwini.” Ndipo ine ndinati, “Tsikulina. . . Magazi amenewo akugwira mkwiyo wa Mulungu kwa iwe. Iwe udzafa limodzi la masiku amenewa. Ndipo, ndiye, iwe—iwe ndi wa ufulu wosankha wekha tsopano, iwe ukhoza kukana kapena kuvomereza.” Ine ndinati, “Koma tsikulina solo yako idzapita kumeneko, kumene sikudzakhalako chifundo chitatsala. Ndipo ngati iwe ungafe mu machimo ako, iwe waweruzidwa kale, ndipo iwe ukupita ku gehena.”

²⁴⁰ Inu mukudziwa chiyani? Mkazi ameneyo analumpho kuchoka pa mpando umenewo apo mmalo odyerawo. Ife tinali ndi msonkhanu wa pemphero umene inu simunaumvepo mmoyo mwanu, ndipo iye anabwera kwa Khristu. Chinali chiyani chimenecho? Musamawaweruze iwo; awuzeni iwo Uthenga. Iwo ndi odzazidwa ndi ziwanda; iwo ndi achivundi mu dera ili. Iwo amakopedwa kuchokera kuno. Chikoka chathu chimachokera kumwamba. Tiyeni tiwone chimene ife tingachite ndi luso lathu, kuwatengera ena kwa Khristu.

²⁴¹ Atate athu Akumwamba, tikukuthokozani Inu chifukwa cha ubwino Wanu ndi chifundo. Ine ndikupepesa, Ambuye; mwinamwake, anthuwa, ine ndawasunga pano motalika kwambiri. Koma pokhala kutseka kwa misonkhanu yamasana iyi monga chonchi, ine ndimafuna ndiwauze iwo, “ziwanda,” ndipo ine ndadula zochuluka kwambiri za izo pa malo amodzi, mu ulaliki umodzi, koma mwinamwake iwo akhoza kuzitolera izo, apa ndi apo, ndi kumvetsa chimene ine ndimatanthauza. Inu mukudziwa zolinga za mtima wanga, zobweretsera izo.

²⁴² Mulole anthu achoke pano masana ano, ndipo amuna ndi akazi azikawona mayendedwe aliwonse amene iwo akupanga, koma azikakhala okondwa ndi omasuka. Mulole iwo akadziwe kuti Mulungu wawapulumsa iwo. Ndipo mulole iwo ayang’ane kwa Iye, akaiwale tizikhulupiro tonse ndi zinthu zimene zawazungulira iwo, ndipo akakhale mwamtendere ndi moganiza bwino, ndi mowopa Mulungu. Ndipo kenako, Mulungu, pamene Inu mudzafuna kuti muwagwiritse iwo ntchito pa chirichonse, Inu mukhoza kudzayankhula molunjika kwa iwo ndi kuwatumiza iwo kulikonse kumene Inu mukufuna iwo kuti

apiteko kapena chirichonse chimene Inu mukufuna iwo kuti adzachite. Mulole anthu akhale odzichepetsa ndipo akapeze Khristu mu mtima mwawo. Tikhululukireni ife, Ambuye, za zolakwitsa zathu, aliyense wa ife.

²⁴³ Ndipo ife tikudziwa kuti—kuti Satana akupita uku ndi uku ngati mkango wobangula, kulikonse, kulikhira zimene iye angathe, atavala zovala zachipembedzo. O Mulungu, ana osauka aang’ono awa, awoneni iwo, paliponse. Iwo ndi otseguka ndi owonekera kwa anthu. Ndipo ine ndikukupemphani Inu, Mulungu, kuti muwachitire chifundo iwowo, ndipo mupulumutse onse otayika, muchiritse odwala. Ndipo, Mulungu, ife tikuzindikira kuti adierekezi akalekale awa a matenda akubwera pa ana Anu, kuti Inu muli ndi chitetezero chiri pamenepo, kuti chisamalire izo. Ndipo adierekezi onse amene angawapangitse iwo kuti achimwe, Inu muli ndi chitetezero chiri pamenepo, chisamalira zimenezo. Ndipo ine ndikukupemphera kuti Inu mupereke izi mu Dzina la Yesu. Amen.

Ine ndikudabwa ngati pali . . .



PHUNZIRO LA ZIWANDA — DERA LACHIPEMBEDZO CHA53-0609A
(Demonology — Religious Realm)
MAULIKI A PHUNZIRO LA ZIWANDA

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lachiwiri masana, Juni 9, 1953, ku Roberts Park Amphitheater mu Connersville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2021 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org